Mafunso ndi Mayankho

Ine sindikudziwa ndi pati. Iwo—iwo mwina, kapena, iwo akhoza kulemba izo mobwereza. Iwo anati, "Yesaya 4:24." Tsopano, Yesaya 4 ali ndi ndime zisanu ndi imodzi zokha mwa iye, kotero ine ndiri . . . ndipo ine sindikudziwa ngati inu mumatanthauza Yesaya 5:24. Apo amati, "Kodi tanthauzo la Lembalo ndi chiani, ndipo nliti pamene ilo liti lidzakwaniritsidwe, Yesaya 4:24?" Ndipo Yesaya 4 ali ndi ndime zisanu ndi imodzi. Ngati inu mungathe . . . Yense yemwe analemba ilo, ngati inu mungathe kuganiza tsopano, mwina, ndi kulilembanso ilo kachiwiri, ine ndikhoza kufika kwa ilo, inu mwaona. Ine sindikudziwa penipeni pamene inu mumapakamba, "Yesaya 4:24, Kodi tanthauzo la Lembali ndi chiani ndipo nliti pamene ilo lidzachitike?"

2 Tsopano, ine sindikusungani inu motalika. Ine ndiri c . . . chabwino, zikomo inu, m'bale. Ndipo ine ndiri—ine ndiri ndi malo ena oti ndipiteko, ndipo ichi . . . Inu mukudziwa, ine ndinali kuganiza, ine ndinali ndi lemba pano, kapena, mundikhululukire ine, kalata yochokera kwa Bambo Baxter. Ndipo ife tisanayambe pa mautumikiwa mmawa uno, pa izi, ine ndati—ine ndikanafuna kuti inu mu—mupemphere ndi ine kamphindi kokha.

3 Ine—ine ndakhala ndikutuluka kunja kwa mautumiki ndi zolinga zopambana kwambiri kuti ndipite mu—mu mautumiki anga aku tsidya kwa nyanja, mmasiku ochepa okha akubwerawa. Tsopano ine ndalandira kalata yochokera kwa M'bale Baxter, M'bale Cox anaiwerenga iyo kwa ine pa lamya usiku wathawu ndipo anaipereka iyo kwa ine mmawa uno, kuti iwo akuyesera kuikonzanso iyo uko tsopano, kachiwiri. Ndipo ine si—ine sindikudziwa ngati uyo ali Satana akuyesera kundigwiririra ine mmbuyo kapena kuti ndi Mulungu akungodikira kuti nthawi ikhale yabwino. Ine—ine sindikudziwa. Iwo akufuna kuika iyo mmbuyo pang'ono mochepa, ndipo iwo akungoziikabe izo mmbuyo kuyambira Oktobala. Oktobala, Novembala, Disembala, Januwale, pano ili pafupi miyezi inai tsopano pamene iwo aiyika iyo mmbuyo.

4 Ndipo tsopano masomphenya abwera, apa iwo analembedwa umu mu Baibulo ndendende basi chimene chiti chidzachitike; koma ndi liti, ine sindikudziwa. Tsopano, ine ndawauza anthu basi (ndi chikhulupiriro chabwino) chimene iwo anandiuza ine, izo kuti akhale okonzeka pofika nthawi ino.

5 Tsopano anthu akuganiza kuti, ine ndikukhulupirira, kuti ine ndangokhala osaona mtima pa izo, "O, bwanji . . . ndi liti pamene iye ati akatenge . . . Ndi liti pamene iye ati apite?"

6 Koma pamene ine ndilandira makalata awa ndipo iwo amandiuza ine, "Chabwino, inu simungakhoze kuchita izo panobe, pali ichi chiyenera kuti chichitidwe, ndi ichi chiyenera kuti chichitidwe." Ndiye ine sindi . . . Ine—ine ndimamverera moipa, ndikamawayang'ana anthu. Ine sindidziwa choti nkuchita. Koma chinthu chimodzi, ine ndichita ichi, ndipo inu nonse limodzi nane; ine ndizipereka izo kwa Mulungu, ndi kuti, "Tsopano, Ambuye, pamene Inu mukonzeka, ine ndiri." Mwaona? Ndipo ngati ine basi . . .

7 Nthawizina imakhala mipingo imachoka pa malo, tsopano ndi zitupa kapena chinthu chinachake. Inu mukudziwa, pangokhala zinthu monga choncho. Uyo akhoza kukhala ali Satana akuyesera kuti achite izo. Chotero pamene ife tikupemphera mmawa uno . . . Ndipo nthawi iliyonse pamene inu muzipemphera podutsa msabatali, inu—inu mundipempherere ine ndi kumufunsa Mulungu kuti . . . Ngati uyu ali Satana, kuti amuchotse iye pa njira. Mwaona? Ndipo ngati ndi—ndipo ngati chiri chifuniro Chake, andigwirire ine kuno. Mwaona? Iye amadziwa ndendende basi choyenera kuti uchite. Mwina pali chinthu china Iye akuzungulira nacho, kufikitsa chithunzi polondola. Ine sindimakufuna konse kupita patsogolo pa Iye. O! Pamene iwe uchita izo, izo nzoopsya. Mwaona? Chotero ine—ine ndikungomverera kuti ndi . . . kuti—kuti icho mwinamwake . . . Ine sindikudziwa choti ndinganene, chifukwa ine sindikudziwa.

8 Basi monga m'bale wathu wokondedwa, George Wright. Ambiri a inu mukudziwa zikhalidwe zake, sichoncho inu? Ndipo inu mukudziwa madokotala amulephera iye, kuti iye anayenera kuti afe sabata lapitalo, kapena kupitirira, mwaona, M'bale George Wright. Ine ndinapita uko kukamuona iye, ndipo ndiri kumeneko ine ndinapemphera ndi kupemphera modzipereka monga ine ndinadziwira kumupempherera kwake iye. Ndiyeno pobwerera kunyumba ndipo ine ndinkadabwa chomwe chikanati chichitike. Ndipo atapita masiku pang'ono, chabwino, ine—ine ndinali ndi masomphenya Lolemba lapitali mmawa, ndipo akuyembekezera . . .

9 Tsopano, pali—pali mkazi amene ine ndinamupempherera anali ndi khansara, ndipo ine ndinamuona iye ataimirira ndipo iye—iye anali . . . Iwo anamung'amba iye, iye anali atangodzaza ndi khansara, iwo anangomusokanso iye. Mwaona? Koma iye akhala moyo. Ine ndikudziwa izo.

10 Koma, tsopano, M'bale George Wright, ine sindinawamvetse bwinobwino masomphenyawo. Ine ndinali kubwera . . . masomphenya omwewo, ine ndinali kutuluka ndipo ine ndinaona ake—malo ake, nyumba yake. Ndipo ku mbali ya kudzanja lamanzere kwa nyumbayo kumene mitengo iyo inali itayima, mtengo wa nkhadze, motsatira kumene pamtunda pake ine ndinaona mabulumwa ena adothi, pafupi kukula ngati chibakera changa, akugudubuzika pansipo. Ndipo ine

ndinamumva Mngelo uyo amene anali ataima cha pambali panga, ananena chinachake cha manda ndi M'bale George.

11 Tsopano, chinali mwina ichi, kuti awo anali manda a M'bale George amene iwo anali kuwakumba, kapena izo zikuwoneka kwa ine . . . Tsopano, kumbukirani tsopano, ine sindikanati ndifotokoze izi . . . ndipo popeza ine ndikukhulupirira kuti ife tiri ndi zothandizira Kuyankhula Kugulu zikudutsa kupyola muno, kapena makina ojambulira, kani. Koma tsopano ine ndikufuna kuti ndipange icho mwachimvekere, monga ine ndinachitira kwa iwo, ine ndikuganiza izo zinali izi . . .

12 Uko kunali kagulu ka anthu kumusi uko amaseka pa iye chifukwa chakuti iye amakhulupirira kuti Mulungu akanamuchiritsa iye dokotala atanena kale, "Iye akudwala. Chabwino, iye sangakhoze, mwaona, magazi aumirira kale mu mapapo ake, ndipo akulavula magazi, ndi china chirichonse." Iye anati, "Kanjere kakang'ono koyamba kokha kakapita ku mtima wake kapena kumutu wake, iko kakanati kadzamupuwalitse iye kapena kumupha iye." Mwaona? Ndipo iye ali ndi zaka seventethuu zakubadwa, wapyola nthawi yoikidwayo.

13 Koma ine ndikukhulupirira kuti izo zinali izi, kuti iye akanadzakumba manda a ena a iwo amene ankamuseka iye, kukumba manda. Ndipo tsopano, ine sindimadziwa kuti iye anali wokumba manda, koma nchomwe ali. Ine, mwaona, pamene ine ndinaganiza kuti, iye amakumba manda, icho nchimene iye amachita. Ndipo izo zimawoneka ngati panali chinachake chokhudza manda ndi kukumba manda, kapena—kapena chinachake chonga izo, kapena—kapena chinachake chonga izo, ndi M'bale George Wright.

14 Ine ndawapempha Ambuye tsopano, kwa pafupi mausiku anai, kuti awabwereze iwo kwa ine kachiwiri ngati Iye angatero. Iwo anabwera motsatira pafupi mma seveni kapena eyiti koloko mmawa wina. Kotero ine ndikudalira kuti Iye adzachipanga icho kumveka. Koma ine ndikukhulupirira ndi mtima wanga wonse . . . Tsopano, ichi changokhala kuti ine ndinali kulondola pamene ine ndinanena kuti iye adzakumba manda a enawo amene anali kumuseka iye, ngati ine ndinawatenga iwo momveka. Koma ine sindiri wotsimikiza kwambiri pa izo. Iwo anali a chinachake cha kukumba manda, ndi M'bale George Wright. Ine ndikuganiza kuti iye anali woti akumbe manda a winawake amene ankamuseka iye.

15 Tsopano, Mulungu ndi chikondi, ndipo, o, ife timangomukonda iye ndi mitima yathu yonse.

16 Tsopano, mmawa uno ife sitikufuna kuti titenge nthawi yathu yochuluka kwambiri muno pa mafunso awa. Ine ndiwayankha iwo mwa kupambana kwa kudziwa kwanga. Tsopano, abwenzi, ine ndikhoza kupanga zolakwitsa zambiri pa zinthu izi. Ndine basi—ndine basi munthu monga ena tonse

a ife. Ndipo M'bale Neville, kapena aliyense wa azilaliki ena awa, kapena ena otero, akhoza kuwayankha iwo mofanana basi monga ine ndikanakhozera. Koma, ine ndimachita izi kwa cholinga, kukhala ngati ndipeze chimene chiri pa mtima wa anthu.

17 Ndiye ngati ine ndiona anai kapena asanu akukoka pa chinthu chimodzi, ndiye ine ndimaganiza, "A-o, ife tiri apa. Pamene, ine ndimadziwa pamene inu muli tsopano, mafunso ena aang'ono mu mpingo." Ndipo tsopano tiyeni tingoiwala za m—mafunso aang'ono. Ndipo chinthu chachikulu pamwamba pa chirichonse ndi kuti tiwusunge mpingo mu chiyanjano ndi mu chikondi cha Mulungu, ndi kumayendabe chitsogolo, ngati ife tonse tingakhoze kukhulupirira kuti Magazi a Yesu Khristu amatiyeretsa ife ku tchimo lonse ndi kusalungama. Ngati mkazi yemwe wakhala pafupi ndi inu, kapena bambo wakhala pafupi ndi inu, ngati iye sakhulupirira kuti Yesu adza—adzabwera kwenikweni mowonekera kachiwiri, tiyeni tingogwirizana ndi-. . . kumapitabe chitsogolo mulimonse. Ife sitikugwirizana naye iye pa Lemba. Koma tiyeni ife tiupange mpingo uzisuntha chitsogolo ku chiyanjano, chifukwa mkati umo ife tikagwiramo anthu ena ochulukirapo. Koma pamene mpingo wachoka mu chiyanjano, ndiye inu—inu mumaupweteka mpingo, ndiye inu mumapweteka cholingacho. Inu. . . icho chiri basi. . . inu simungakhoze basi kuchita izo. Koma pamene ife tingakhoze kugwirizana pa chinthu chimodzi, kuti Magazi a Yesu Khristu amatiyeretsa ife ku tchimo lonse (uko nkulondola) ndipo tchimo lachoka, ndiye ife—ife tiri pafupi kwambiri ndi mzere wa kwathu ndiye, M'bale Neville. Pamene Magazi, pamene tiri Maga-. . .

18 Ine ndiri naye m'bale, ndife abale mwamagazi. Koma, mai, momwe ife sitimagwirizanirana; nhu, momvetsa chisoni. Koma, chimodzimodzi basi, ndife abale.

19 Tsopano, ine ndinali kuganizira za sabata lino, sabata likudzali, ngati ine sindipita kutsidya kwa nyanja, mwina. . . M'bale Cobbles abwera kuno, ndipo iye ankafuna kuti ayambe kukopa anthu mu Louisville, ndipo iye amafuna kutenga Zida poti ife tinali ndi kamsonkhano kathu kakang'ono kamachiritso kumeneko usiku wina. Ndipo Ambuye anachita zinthu zina zodabwitsa. Ndipo chotero. . . Koma ndiye ine ndinapeza kuti abale awo ochokera ku Del Rio, Texas, a Jessup achibale, ali ndi msonkhano mu Louisville ndipo iwo ali naye woyankhula wao wabwino zedi kumeneko kwa masabata otsatira akudzawa. Ndipo anati iye samadziwa ndi liti pamene iye ankati achoke. Charles, ine ndikhulupirira ndi yemwe ali, ndi amene ati akhale kumeneko sabata imene ikudzayi, ndipo ine ndithudi sindikanati ndiyambe chitsitsimutso kwina kulikonse ndi kukopa kwa mtundu umenewo kukuchitika.

20 Ndipo iwo alinso ndi kukopa kwamachiritso. Ndipo

chotero kukopa kwamachiritso kuli madzulo, madzulo ano. Ndipo chotero ine sindikanafuna kuyamba msonkhano ndi—ndi iwo ali ndi msonkhano uko, chifukwa ine ndimadziwa chimene chiri kukhala uli kwinakwake ndipo izo basi . . . O, inu mukudziwa, pamene ine ndikuchititsa msonkhano ndipo wina nkulumphirapo ndi kuyamba kamsonkhano kakang'ono konga ako. Izo sizimawoneka bwino basi, izo sizimazipatsa izo malo abwino, inu mukudziwa. Chotero ife tingodikira mpaka mtsogolo pang'ono, mwina Ambuye atithandiza ife. Iye atithandiza ife, mulimonse, ndipo kotero ife tingokhulupirira ndi kugwiritsabe ndi kukhala okhulupirika kwa Mulungu.

Tsopano tiyeni tipemphere:

21 Atate, Kumwamba, mulole madalitso Anu awalire pa ife tsopano pamene ife ndikupita patsogolo kuti ndiyankhe mafunso awa. O Mulungu, basi . . . Alipo ena a iwo pano ine sindinawayang'ane nkomwe ngakhale panobe, ndi awiri kapena atatu okha amene ine—ine ndinawerenga kanthawi kapitako basi. Ine ndikupemphera, Atate, kuti Inu mundithandize ine ndi kundipatsa ine nzeru ndi kumvetsa, kuti ine ndingoyankhula icho chomwe chiri cholondola. Perekani izi, Atate. Ndipo mulole ine ndikhale ndi Nzeru Yanu ndipo mulole Mzimu Woyera udze pansi pakali pano ndi kupereka nzeru yomwe ikusoweka. Tidalitseni ife limodzi lero, Ambuye, monga gulu laling'ono la kachisi uyu pano.

22 Mumdalitse m'bale wathu wabwino wokondedwa, M'bale Neville, pano, Atate, iye akuvutikira mopitirira, m'busa pano mu munda wa msipu, yemwe—yemwe akuyesera kutsogolera nkhosa ku msipu wobiriwira ndi zipaso zakuya, kapena kunja mkati mwa madzi ndiyeno nkubwerera ku mtengo wamthunzi, ndi kumasamalira odwala ndi osowa ndi opunduka aang'ono ndi iwo amene ali otopa ndi kuyesera kuwapatsa chithandizo cha dotolo iwo ndi kuwabweretsa iwo, kuti iwo akhale nkhosa zenizeni. O Atate, ine ndikupemphera kuti Inu mumudalitse iye. Mpatseni iye nzeru ndi chidziwitso ndi kumvetsa.

23 Ndipo tithandizeni ife tonse palimodzi tsopano, Atate, ndipo ife tikupatsani Inu mayamiko. Mu Dzina la Yesu. Ameni.

24 Tsopano, mu ena a awa apa, ine ndiwatulutsa iwo, ine ndiwasanjika iwo mumagawo basi a Lemba pamene iwo—pa malo ake. Ndipo tsopano ife tingoyamba pa ena, ndi kuyankha motsatira kumene mpaka ife tikhoze kungowatenga—kutenga ambiri momwe ife tingakhozere kuwatha. Ndipo ine ndikukhulupirira ife tikhoza kuwatenga iwo onse, ndipo ine ndikhala ngati ndikuyang'ana apa kuti ife tituluke mofulumira.

25 Chinthu choyambirira ndi funso chabe, funso lolunjika basi:

8. Ine ndinabatizidwa pa usinkhu wa khumi ndi zitatu. Kodi ine nditero kachiwiri?

26 Tsopano, ilo ndi—ilo ndi funso laling'ono labwino kulifunsa. Chabwino, tsopano, mzanga, ine nthawizonse ndimazisiyira izo kwa munthuyo.

27 Kumbukirani, ine sindikudziwa . . . Pali limodzi limene ine ndikulidziwa yemwe analilemba ilo, ilo ndi limodzi ili pomwe pano, ndipo bamboyo analipereka ilo kwa ine yekha. Ndipo wina anandifunsa ine funso kumbuyo uko kuti ine ndiliyankhe, ndipo iwo sanaliyike ilo konse pa pepala, ndipo ine ndinati, "Ngati ine nditi ndikhale ndi nthawi yokwanira ndikatha awa pano ine ndikadaliyankha ilo."

28 Koma tsopano ili pano "Kodi ine . . . Ndinali ine . . . "

Ine ndinabatizidwa ndiri khumi ndi zitatu. Kodi ine ndidzabatizidwe kachiwiri?

29 Ngati inu mwakhala muli Mkhristu nthawi yonseyo, kuyambira inu muli ndi zaka khumi ndi zitatu, wokhulupirira mwa Khristu, ine—ine ndikanangokhala momwe inu muliri. Ine sindikadatero tsopano, ngati Mulungu wakudalitsani inu ndi kukupatsani inu Mzimu Woyera kuchokera apo.

30 Ndipo ubatizo uli kokha m—m—maonekedwe, iwo uli chabe u—uliwonetse dziko (kapena osonkhana omwe inu—inu muli nawo pa nthawi imeneyo) kuti inu, pamaso pa mboni, mukutsimikizira kuti inu mwakhulupirira kuti Mulungu anatumiza Mwana Wake ndipo Iye anafa ndipo anauka kachiwiri pa tsiku lachitatu, ndipo inu munaikidwa mwa Iye ndipo mwauka kuti muziyenda mwa utsopano wa moyo. Ndipo anthu omwewo amene anakuonani inu pamene inu munali kubatizidwa adzakumana nanu pa chiweruzo. Mwaona?

31 Ndiyeno popitirira, ngati wina (mlendo) anena, "Kodi inu?"

32 "Inde, ine ndinabatizidwa ndi wanga . . . ku imfa ndi kuikidwa mmanda kwa Ambuye wanga."

33 Mwaona, ine ndikuganiza kuti ubatizo . . . O, ine ndikunena kuti ndi wofunikira, ine sindikadafuna kunena kuti iwo suli wofunikira. Koma iwo ndi wofunikira pakuti iwo uli . . . Lamulo lirilonse la Mulungu ndi lofunikira. Kodi inu simukuganiza choncho? Ziri zofunikira kuti ife tizibatizidwa. Yesu anapereka neno ili mu Mateyu Woyera, kapena Marko Woyera 16, Iye anati, "Pitani mu dziko lonse ndi kukalalikira Uthenga, iye amene akhulupirira ndipo akabatizidwa adzapulumutsidwa." Ndipo pamene Iye anali kuyankhula kwa Nikodimo, Iye anati, "Kupatula ngati munthu abadwa mwa madzi ndi Mzimu iye sadzati mwanjira iliyonse adzalowe." Mukuona? Iye ayenera kuti abatizidwe. Ine ndimakhulupirira kumiza, mu ubatizo, mu Dzina la Ambuye Yesu Khristu, ndi kuti awukitsidwe kachiwiri mu utsopano wa moyo, kuti aziyenda motsatira Malamulo a Mulungu.

34 Koma, inu mukuti, "M'bale Bill, kodi inu munayamba mwamubatiza wina aliyense, amene anabatizidwapo pamene iwo anali mwana wamng'ono ndipo tsopano nkubatizidwanso?" Nthawi zochuluka.

35 Apo—pali Lemba uko mu Chivumbulutso, mutu wachiwiri, akuyankhula kwa mpingo, Iye anati, "Lapani ndi kumachita ntchito zako zoyamba mobwerezanso." Ndipo ambiri a iwo anatanthauzira Lemba ilo kumanena izi, kuti izo zikutanthauza inu mukuyenera kupita kumbuyo komwe ndi kukachita chinthu chomwecho mobwereza. Chabwino, ngati inu mungazindikire, bwenzi lokondedwa la Chikhristu . . .

36 Tsopano, ine sikuti ndikutsutsana ndi izi tsopano, mwaona, chifukwa ife tiri ndi mobatizira modzaza. Ife tiri okonzeka kuti tibatize aliyense yemwe akufuna kuti abatizidwe pa nthawi iliyonse. Koma ife sitiri kutsutsa. Ngati inu mukufuna kuti mubatizidwe, ngati icho chiri chinachake chimene chikuima mu njira yanu ndipo inu mukumverera ngati inu muyenera kutero, inu mupite mukachite izo. Ndiko kulondola. Inu mupite mukachite izo. Musati mulole chinthu chirichonse chiime mu njira yanu, inu mudzipange nokha wokonzedwa mwangwiro.

37 Basi monga—ngati inu munatenga chinachake, zaka zapitazo, ndipo inu mukumverera ngati inu muyenera mupite kukazikonza bwinobwino izo, inu pitani mukachikonze icho molondola. Ziribe kanthu chomwe icho chiri. Inu zonse zikhale bwino bwino. Chifukwa inu mudzabwera mpaka ku chinthu chomwecho, ndipo inu simungakhoze kupita patali kulikonse mpaka inu mutachichotsa icho panjira, inu mukuona. Inu mukuyenera basi kuika pambali cholemetsa chirichonse ndi chinthu chomwe chimaku fooketsani inu mophweka.

38 Ndipo ngati inu mukufuna kuti mubatizidwe kachiwiri, pitirirani kutero, ndicho chinthu choyenera kuchichita. Ine ndawabatizapo kachiwiri ambiri.

39 Koma tsopano ku Lemba ilo limene inu mukulozerako, ilo silinali kuyankhula kwa payekha, ilo linali kwa mpingo. Mwaona, mpingo, chomwe iwo anali atachita, iwo anali atataya chikondi chawo choyamba, mwaona, chozuna chenicheni chomwe iwo anali nacho pachiyambi. Ndipo Iye anati, "Pokha inu mutalapa ndi kumachita ntchito zoyamba izi kachiwirinso," kayambireni mmbuyo momwe ndi kukapeza chinthucho. Iye ali kuyankhula kwa mpingo, "Pokha inu mutalapa ndi kubwereranso kachiwiri," chabwino, ndiye, Iye amati achotsapo choikapo nyali.

40 Ndi monga ngati inu mukufuna kuti mubatizidwe, ndipo ngati inu munabatizidwa pamene inu munali khumi ndi zitatu, kapena usinkhu uliwonse, bwanji, inu—inu mubatizidwe ngati icho chiri kukutchingani.

41 Koma tsopano kuti tinene izo Mwamalemba ine ndikhoza kunena kuti inu muyenera kuti mubatizidwe kachiwiri, pali njira imodzi yokha ya Mwamalemba yomwe ine ndingakhoze—ndingakhoze kulengeza kuti anthu anabatizidwanso. Pali Lemba limodzi lokha mu Baibulo lonse pamene anthu anabatizidwanso, ndipo awo anali iwo amene anabatizidwapo ndi Yohane M'batizi Mzimu Woyera usanabwere. Paulo, mu Machitidwe 19:5, anawauza iwo kuti iwo anayenera kuti abatizidwenso kachiwiri mu Dzina la Yesu Khristu, polinga kuti alandire Mzimu Woyera. Mwaona?

42 Tsopano—tsopano, iwe sumasowa kuchita kubatizidwa kuti ulandire Mzimu Woyera, chifukwa iwe ukhoza kuulandira Mzimu Woyera pamene mtima wako uli moyenera. Mwaona? Chifukwa, pa Machitidwe 2, Petro anapereka dondosolo kuti—dongosolo kuti, "Lapani, ndipo mubatizidwe mu Dzina la Yesu Khristu, ndipo inu mudzalandira mphatso ya Mzimu Woyera." Komano, mu Machitidwe 10:49, Mulungu anatembenuka apo ndipo anawapatsa Amitundu ubatizo wa Mzimu Woyera iwo asanabatizidwe nkomwe. Inu mukuona? Chotero, inu mukuona, ndi momwe mtima wako uliri.

43 Ndiye Petro anati, "Kodi ife tingakhoze kuletsa madzi, powona kuti awa alandiranso Mzimu Woyera monga ife tinalandira iwo pa chiyambi?" Inu mukuona? Chotero ndiye iye—iye anawaumiriza iwo kuti iwo ayenera kuti abatizidwe mu Dzina la Yesu Khristu.

44 Ndiye Paulo, mu Machitidwe 19, anati . . . Paulo, atadutsa ku magombe akumtunda kwa Efeso, iye anawapeza ophunzira ena, ndipo iye anati kwa iwo, "Kodi inu munalandira Mzimu Woyera kuchokera pomwe munakhulupirira?"

45 Iwo anati, "Ife sitikudziwa ngati . . . sitikudziwa ngati kuli Mzimu Woyera uliwonse."

Iye anati, "Kodi inu munabatizidwira kwa chiani?"

Iwo anali. Iwo anati, "Ife tinabatizidwira kwa Yohane."

46 Iye anati, "Yohane ankabatizira ku kulapa, kumanena kuti 'Inu munayenera kukhulupirira pa Iye woti abwereyo,' monga pa Ambuye Yesu Khristu." Ndipo pamene iwo anamva izi, iwo anabatizidwa kachiwiri mu Dzina la Yesu Khristu. Mwaona? Kotero ndiye ndicho . . .

47 Tsopano, pa ichi, chiri . . . Koma kungonena kuti inu munabatizidwa mu ubatizo wa Chikhristu pa usinkhu wa satini, ndipo inu mwakhala moyo wa Chikhristu njira yonseyo motero, kapena ngati inu munabwerera mmbuyo nthawi zingapo . . .

48 Ine sindikudziwa ngati iwo apeza . . . pa kubwerera mmbuyo, ine sindikudziwa, nkadakonda wina akanati amke nandifunsa—kundifunsa ine izo. Koma pa kubwerera mmbuyo, kumbukirani, inu mumabwerera mmbuyo tsiku lirilonse. Palibiletu njira

nkomwe yoti inu mulewe izo ayi. Chabwino. Koma inu mumabwerera mmbuyo kwa anthu mu mpingo, koma osati pamaso pa Mulungu. Mwaona? Inu mumabwerera mmbuyo pa Khristu, koma inu simutero pa Mulungu. Chifukwa, ngati inu mukanakhala kuti, Pamene inu mwachimwa, inu mwapita. Koma inu mumagwa mowirikiza. Paulo ankachita kumafa tsiku lirilonse. Ndi kulondola uko? Iye ankachita kumafa tsiku lirilonse, kulapa tsiku lirilonse, ndi basi mowirikiza kumalapa nthawi zonse. Mukuona? Ndipo ngati Paulo ankayenera kuti azichita izo, ndiye ine ndiyenera kuti ndizitero, nanenso. Sichoncho inu? Ndiko kulondola. Chotero ife . . .

49 Koma tsopano, ngati—ngati inu mwakhala—ngati inu mwakhala mutaomboledwa ndipo inu mukumverera kuti—Magazi a Yesu Khristu anakuyeretsani inu ku tchimo, ndiye ine—ine. . . ndipo inu mwakhala moyo wa Chikhristu, ine—ine sindikadaganiza izo zikadakhala zofunikira. Koma ngati inu mukufuna kutero, chabwino, izo zikhala zabwino, ife tikhala osangalala kuti tichite izo.

50 Tsopano pano pali kolembedwa kakang'ono kamene winawake anandipatsa ine kumbuyo uko:

9. Kodi ndi malo otani omwe mpingo uti udzakhale ulimo pamene Uthenga ukubwerera kwa Ayuda?

51 Tsopano, munthu amene anachita izi, anali kulozera pano ku Luka, i. . . Iye—iye anandiuza ine, m'bale wathu, kuti iye anali kulozera pamene Ilo linati, "A—Amitundu adzapondereza makoma a Yerusalemu mpaka nyengo za Amitundu zidzakhale zitatha." Izo ndi mu Luka 21:24. Tsopano mvetserani mwatcheru ndipo ichi chikhoza kuzipeza izo. Funso lokongola? Zodabwitsa!

> *Ndipo pamene inu mudzaona Yerusalemu atazingidwa* mozungulira *ndi ankhondo, ndiye dziwani kuti chipululutso chake chayandikira.*

52 Tsopano, tiyeni ife tichigwire ichi mofatsirira tsopano. "Chipululutso chiri pafupi pamene inu mudzaona Yerusalemu atazingidwa mozungulira ndi ankhondo." Tsopano, icho chakhala chiri chosokoneza kwambiri apo, ndi anthu mu. . . . Koma muziyandikira ichi kuchokera mmaimidwe a mbiriyakale ndi Baibulo.

53 Tsopano, abale a Adventisti, abale a Seventh-day Advent, iwo amakhulupirira kuti—kuti Yerusalemu adzazingidwa kachiwiri mozunguliridwa ndi ankhondo. Chabwino, tsopano, izo zikadakhoza kukhala zoona, pakuti Lemba liri ndi matanthauzo apawiri nthawi zambiri.

54 Ndipo ndi angati amadziwa kuti Lemba liri ndi matanthauzo apawiri kwa uneneri uliwonse? Zedi liri! Inde, bwana. Ilo limanena ichi ndi kutanthauza ichi ndendende basi ku nthawi *iyi*, ndi kutembenuka apo pomwe ndi kudzachibwereza icho kachiwiri mmbuyo cha *apa* kwinakwake. Mwaona?

Monga . . . Ndipo ine ndilozera kwa amodzi mwa iwo ngati ine ndingakhoze kuganizira za iwo mwamsanga kwambiri. O, inde, pano pali amodzi mu Luka . . . Mu Mateyu 2, anati, "Ndipo Yesu anaitanidwa kuchokera ku Igupto kuti chikhoze kukwaniritsidwa chimene chinayankhulidwa ndi mneneri, kuti, 'Wanga . . . Ine ndaitana mwana Wanga kuchokera ku Igupto.'"

55 Tsopano, uneneri uwo, ukulozera mmbuyo umo ndi mneneri, unali ndendende wolozera kwa *Israeli* (amene anali mwana wa Mulungu) Iye anamuitana kuchokera ku Igupto. Ndiko kulondola, mu—mu Genesis, Eksodo. Koma una—unali kulozeredwa ku—kumeneko, koma unadzabwerezedwa kachiwiri. "Kuchokera kwa Lako . . ." Israeli anali mwana wa Mulungu. Inu mukuzidziwa izo. Iye anamuuza Farao, anati, "Iwe . . ." Ananena kuti, "Iwe—iwe . . ." Chimene iye anachita kwa Mwana Wake, kuti Iye akanati adzatenge moyo . . . Iye sakadati amulole mwana Wake kuti apite, chotero Farao . . . Mulungu anatenga Mwana wa Farao kuchokera . . . ndi . . . kapena mngelo wa imfa usiku uja. Kotero ndi tanthauzo lapawiri.

56 Ndipo chotero, tsopano, monga Yerusalemu, anazingidwa ndi ankhondo, koma, kwenikweni, mwa mbiriyakale, izo zinali mu pafupi a.d. 96 pamene Tito anazungulira Yerusalemu. Koma tsopano penyani ichi mwatcheru, inu mukhoza kuona chosiyanitsa, ine ndikukhulupirira kuti Yerusalemu adzazingidwa mozunguliridwa ndi ankhondo kachiwiri pa nthawi yotsiriza. Koma ine ndikukhulupirira ichi apa chinali kufanizitsa ndi pamene Tito anauzungulira iwo, pamene chipululutso chakecho.

57 Tsopano, "Chipululutso," tikunenachi . . . chinali pamene Daniele, mneneri . . . "kuima mu malo Opatulika." Zindikirani, iye anati, "Pamene inu muona chonyansa chimene chikupangitsa chipululutso chitaimirira mu malo Opatulika." Mwaona, "chonyansa," *chonyansa* ndicho "kusayera." "Chimene chikupangitsa chipululutso," *chipululutso* ndicho "kuti uthane nazo," ndi kuti "uwononge." "Pamene inu muona chonyansa chimene chikupangitsa chipululutso chitaima mu malo Opatulika," zinakwaniritsidwa mwamalemba pamene Tito anazinga Yerusalemu, anatenga . . .

58 Mwa kuyamba kwa mutu uwu pamene iwo anali kumufunsa Iye, "Ndi liti pamene nthawi yachimaliziro iti idzakhale? Ndipo zidzakhala chiani zizindikiro za kudza kwa . . . kwa Khristu?" Ndipo iwo anamuuza Iye za kachisi, momwe iye analiri, mwaubwino momwe iye analiri atakomeretsedwa ndi miyala yaikulu ndi zinthu.

59 Iye anati, "Padzafika nthawi imene sipadzakhala pali ngakhale mwala umodzi utasiyidwa pamwamba pa umzake, kuti iwo adzagwetsedwa pansi." Iye anayamba kuwapatsa iwo

zizindikiro ndi zodabwitsa. Ndiye, Yesu akuyankhula tsopano, akutembenukira tsopano kwa Daniele, kuti akwaniritse, chifukwa uneneri wonse uyenera kulumikizana umodzi ndi umzake. Lemba lonse ndi losathyoka pena paliponse.

60 Yesu anati, "Malemba sangakhoze kusweka." Ameni. Ndi apo . . . Kodi ine ndikupita Kumwamba? Zedi, ine ndiri! Malemba sangakhoze kusweka. Kwa inu amene simumakhulupirira mu zizindikiro ndi zozizwitsa ndi zodabwitsa, kodi inu mungakhoze bwanji kuchoka kwa Lemba limenelo? Malemba sangakhoze kusweka, mosapambana momwe Khristu angakhozere (pamwamba pake apa), angakhoze kuthetsedwera. Basi monga thupi Lake lalikulu mmwamba, ndipo kusuntha kulikonse kwa thupi Lake kumanyezimiritsa kuyenda kwa pansi pano padziko, ili liyenera kuti litero. Ndiye ngati Khristu . . . ngati anu . . . machiritso Auzimu, mphamvu ya Mulungu yachotsedwa kwa mpingo weniweniwo, kapena mpingo wauzimu pa dziko lapansi pano, ndiye iyo yachotsedwa kwa Khristu. Iye salinso . . .

61 Koma, o, ndi chithunzi bwanji cha Mpesa woona pamenepo, ndipo ife ndife nthambi mu Mpesa umenewo. Mwaona? Basi momwe Mpesa ukusunthira, ndimomwe nthambi zimasunthira. Ndi kulondola uko? Kukongola kwake tsopano momwe thupi Lake lalikulu, o, mikono Yake yaikulu youkha magazi ndi misozi yokugwa, ndi mbali Zake zoukha magazi, ndi msana wake wokwapulidwa utapachikidwa pamwamba pa dziko monga *chonchi* pakati pa Mulungu (Atate) ndi zivundi za dziko lapansi ili, a-kuchonderera ndi kuwakonda iwo basi pamene thupi Lake likudza poyenda ndi mphamvu, iyo yaperekedwa mu Mpingo.

62 Basi monga Iye atati, "Ine ndigwedezera manja anga mbali iyi," ndipo thupi Lake lenilenilo limasuntha. "Ndipite uko ndi kukalalikira Uthenga," inu muuwona Mpingo ukusuntha molunjika ndithu. Chifukwa, mthunzi wanga uyenera kumasuntha ndi dzanja langa. Ameni. Ndi kulondola uko? Ameni. O, mai, pamene ine ndiganiza za izo! Ndi ilo apo, Thupi Lake likusuntha, "Pitani inu mu dziko lonse, mukaonetsere Mphamvu." Ziribe kanthu ngati ife tiziyendera pa zamulungu zathu ndi zophunzitsa ndi zina zotero monga choncho, ife timalephera mowawa. Koma tsopano dzanja la Mulungu liri nkusuntha, zizindikiro ndi zodabwitsa zikuonekera. Bwanji, mai!

63 Yesu ananena, kumeneko pamene Iye anali kutululutsa ziwanda . . . Osati kuchoka ku funso ili, tsopano, kwa kamphindi kokha. Koma Yesu ananena, pamene Iye anali kutululutsa ziwanda, Iye anati, "Kodi ana anu amazitulutsa izo ndi chiani?" Ngati Ine ndi chala cha Mulungu ndikutululutsa ziwanda, ana anu amazitulutsa izo ndi ndani? Ngati inu muli ndi upangiri wabwinopo, tionetseni ife." Mwaona? "Ngati Ine ndi chala cha Mulungu . . ." Ameni. Tangoganizani, "chala" cha Mulungu.

Pali Mulungu pamwamba pa Khristu; Khristu pamwamba pa mpingo. Pali Mulungu, Atate, akanena chinthu *chakuti-chakuti*; ndiye Mulungu, Mwana, amasuntha dzanja Lake ndipo chithunzi chimatsatira izo. "Ngati Ine ndi chala cha Mulungu ndikutululutsa ziwanda, ana anu amazitululutsa izo ndi ndani?"

64 Penyani, ine ndikufuna inu muzindikire. O, ziribe kanthu momwe matenda aliri aakulu kapena momwe chisautso chachulukira Mdierekezi angakhoze kuchiyika pa inu, zimangotengera chala Chake kuti azisunthe izo. O, mai! Mai! Tapenyani pa mapewa amphamvu awo ndi mikono ndi akatumba. Chala Chake chokha chimatulutsa nthenda iliyonse ndi kutululutsira kunja ziwanda. Ndi kanthu kakang'ono bwanji komwe Mdierekezi ali! Iye amangotenga chala Chake ndi kumusunthira iye kutali ndiye. "Ngati Ine ndi chala cha Mulungu. . . "

65 Tsopano ndiroleni ine ndikuonetseni inu chikondi china cha Mulungu. Koma pamene nkhosa inataika, Iye sanagwiritse ntchito chala Chake, Iye anamuika iye pa mapewa Ake, ndipo iye anatenga Uthunthu Wake wonse, manja, nkhosa ili pa phewa Lake. Gawo lanyonga, lamphamvu kwambiri la munthu ndi kupingasa pa mapewa ake ndi pansana. Inu mukudziwa izo. Pakuti akatumba ake onse a mkono ndi akatumba amasunthira kunja, ndipo Iye amaitenga nkhosa yonseyo; kuiyika Iyo pa phewa Lake ndipo apa Iye akubwera, osati ndi chala Chake, kuti atulutse kachiwanda kakang'ono, kakaleko, koma apa Uyu akubwera ndi Ake. . . akatumba Ake onse a mwendo Wake, akatumba onse a mkono Wake, akuyenda kudutsa mchipululu, atanyamula nkhosa yotaika pa phewa Lake. O, mai! "Ngati Ine ndi chala cha Mulungu ndikutululutsa ziwanda, ana anu amatulutsa izo ndi ndani?" O, aleluya! Mai!

66 Chabwino, tibwerere ku phunziro:

> Koma *pamene* inu. . . *mudzaona Yerusalemu atazingidwa* mozungulira *ndi ankhondo,* . . .
>
> *Ndiye siyani iwo amene ali mu Yudeya athawire* mu *mapiri; ndipo siyani iwo amene ali mkati mwa iwo asapite kunja; ndipo siyani. . . iwo* amene *ali mmaiko alowe* . . . imo.
>
> *Pakuti awa* adzakhala *masiku a—a kubwezera, kuti zinthu zonse zimene zinalembedwa zikhoze kukwaniritsidwa.*
>
> *Koma tsoka kwa iwo amene ali ndi mwana, ndi kwa iwo amene akuyamwitsa, mu masiku amenewo! pakuti kudzakhala kuli chisautso chachikulu mu dziko, ndi mkwiyo pa anthu.*
>
> *Ndipo iwo adzagwa ndi nsonga ya lupanga, ndipo adzatengedwa undende kumka ku mafuko onse:* . . .

67 Zindikirani kukongola kwake apa Lembali liti chipangidwe momwe zinanenedwera. Chinthu choyamba, "Ndi nsonga ya malupanga." Lotsiriza ili lidzakhala ndi bomba la atomiki. Mwaona? Koma izi ndi mwa nsonga ya lupanga, ndipo Ayuda anali oti atengedwere kwina atagwidwa ku maiko onse. Izo sizidzakhala mwa njira imeneyo kachiwiri, iwo adzakhala atasonkhanitsidwa mu Palestina kwa nthawi yotsiriza. Mwaona? Izi zinali kulozera ku masiku amene anapita kale. Ndipo izo ziri basi ndendende molingana ndi mbiriyakale, zinafika pochitika mwa njira imeneyo basi.

68 Iwo anatsogozedwera kutali kumka ku mafuko onse. Fuko lirilonse pansi pa Thambo lero, inu mumapezako Ayuda. O, fuko lirilonse! Inu mukapita ku China, ndipo inu mukawapeza Ayuda. Inu mukapita ku Russia, inu mukawapeza Ayuda. Mukapita ku zisumbu zazing'ono, inu mukawapezako Ayuda. Atamwazikira umo pakati pa fuko lirilonse! Nchiani icho? Uneneri wa Mulungu. Mulungu analinga izo. Ndipo Ayuda amenewo ndi zizindikiro za mtunda, m'bale. Pamene inu muwaona iwo . . .

69 Ine ndikudziwa iwo ali akhungu ndipo atsogoleredwa kutali, ndi kumanyenga ndi chirichonse, koma iwo ananyengedwa ndi Mulungu kuti inu ndi ine tikhoze kukhala nako kupenya. Uko nkulondola. Koma ine ndikunena izi mu mzimu wa uneneri, mwa Baibulo, kuti, ora la Ayuda kuti abwerere kwao liri pafupi. Inde, bwana. Iye anaumitsa mtima wa Hitler, anawathamangitsa iwo atuluke mu Germany; anaumitsa mtima wa Mussolini, anawathamangitsa iwo atuluke mu Russia. Iye akuwathamangitsa iwo kuchokera kulikonse, monga Iye anachitira mu masiku pamene Iye ankawatulutsira iwo kunja. Ndiyeno pamene iwo anakafika uko mchipululu uko ndipo anali okonzeka kuti awolokere uko, nchiani chinachitika? Mulungu analichezera dzikolo ndi miliri yaikulu ndi zinthu. Zomwe Iye ati adzabwerezenso ndi antchito Ake awiri, mitengo iwiri ya azitona ya Ezekiele ndiponso ya Chivumbulutso 11. Iye adzabwereza zizindikiro zimenezo ndi zodabwitsa.

70 Tayang'anani pa mboni ziwiri izo mu Chivumbulutso 11, "Ine ndidzapereka mphamvu kwa mboni Zanga, ndipo izo zizidzatseka miyamba mmasiku auneneri wawo, kapena kutumiza miliri pa dziko lapansi monga iwo afunira." Ndi zimenezotu, mboni ziwirizo mu masiku otsiriza.

71 Ine ndikudziwa kuti kuphunzitsa kwamakono ndi koti, "Izo ndi za Chipangano Chakale ndi Chatsopano." Izo nzolakwika! Izo nzolakwika!

72 Si mboni ziwiri, ndiko mwamtheradi kubwerera kwa Mose ndi Eliya. Ndipo inu mukuzindikira kumbuyo uko, palibe mmodzi wa iwo . . . Mose, iye anamwalira, koma kodi iye anapita kuti? Iye anachita kuuka kachiwiri. Ndipo Eliya anasinthika

ngakhale popanda imfa. Iye adzayenera kuti adzafe, chifukwa wa chivundi aliyense ayenera kutero, chotero iye adzayenera kubwereranso uko kachiwiri. Ndipo apo pali mboni ziwiri.

73 Tsopano, penyani:

> *Ndipo iwo* adzapondereza . . . *Ndipo iwo adzagwa ndi nsonga ya lupanga,* . . . (ndime ya 24) . . . *ya lupanga*, *ndipo* onse *adzatengedwa kwina atagwidwa kupita ku mafuko onse:* ndipo *Yerusalemu* adzaponderezedwa *pansi ndi Amitundu, mpaka* . . . (Ameni!) . . . *mpaka* nthawi *za Amitundu zikhale zitakwaniritsidwa*.

74 Zonjenjemeretsa, si choncho, kudziwa kuti ife tiri ndi nthawi yochepa? Mulungu ananena chomwecho! Nyengo ya Amitundu inalowetsedwamo ndi Mfumu Nebukadinezara. O, kupambana kwake! Nthawi yochuluka yomwe ine ndingataye pa izi, kwa maminiti ochepa okha! Koma zindikirani, aliyense akufuna funso lao. Koma, ife tikadali pa ichi, tiyeni ife tiganizire pa ichi, chifukwa chiri chofunikira zedi tsopano, pakali *pano*.

75 Penyani! Mulungu anawatsogolera anthu, Ayuda. Iwo sanali konse fuko, iwo anali anthu chabe. Ndipo iwo sanali konse mpingo wa bungwe, iwo anangokhala mpingo woitanidwa utuluke. Panalibe konse bungwe pakati pa Ayuda, iwo anali nthawizonse akutsogozedwa ndi Mulungu.

76 Ndiye pamene mwandale, mwafuko, iwo ankafuna kuti akhale . . . akhale nayo mfumu. Ndipo Mulungu anawapatsa iwo mfumu ndipo izo sizinagwire konse ntchito. Mulungu anali Mfumu yao. Mulungu ndiye Mfumu yathu, ndiko kulondola, ndipo Mulungu ndiye Mfumu ya Mpingo.

77 Tsopano, zindikirani ndiye pamene iwo anagwidwa ndipo anatengedwera kutali ku Babeloni chifukwa iwo ankayesera kusanzira mafuko a mdziko. Ndi chithunzi chokongola bwanji lero cha mpingo ukuyesera kusanzira dziko kunja uko, ndi kutengedwera kutali, kutengedwera kutali ndi kwao—kukhala kwao. Mpingo ukukhala mofanana basi monga dziko likuchitira, kumapitiriza, kumachita mofanana basi monga ilo, ndi china chirichonse, ndi kumadzitcha kuti ali Mpingo. Inu simungakhoze kuchita izo. Iai, bwana. Moyo wanu womwe umatsimikizira chomwe inu muli.

78 Chimene inu muli . . . Monga ine ndinanena pachiyambi, chimene inu muli kwinakwake ndi chimene inu mumanyezimiritsa kuno. Chimene inu muli, chimene thupi lanu lakumwamba kapena lapadziko liri kumwamba uko, chimene thupi lanu lakumwamba liri kwinakwake ndi chimene inu mukunyezimiritsa kumbuyo kuno. Mu dziko lauzimu, chimene inu muli, ndi chimene inu muli kuno. Ngati inu mukadali amalingaliro-onyansa ndi zina zotero mu dziko lauzimu, inu muli onyansa-mmalingaliro kuno. Ngati inu mukadali pano ndi nkhwizi, nsanje, ndi makangano, inu muli mu dziko la

mzimu ndi zimenezo, izo zimanyezimiritsa kumbuyo kuno. Koma ngati umunthu wanu wonse wamkatimu wayeretsedwa ndi kukonzedwa, izo zimasonyeza kuti inu muli ndi thupi kutali uko (likudikirira) limene layeretsedwa ndipo lakonzedwa, ndipo ilo likuchitachita mobwereza mu mnofu. Kodi inu simukuona? Mwaona, ndi izo apo. "Ngati msasa uwu wa dziko lapansi ukhala utasungunuka, ife tiri nawo kale wina ukutidikirira." Mwaona?

79 Tsopano, mu nthawi ino, nthawi yotsiriza, momwe kuti kufanizitsa kwa chithupithupi uku, kusanzira kwa Chikhristu zonsezo zidzasakanizikira mu Babeloni mmodzi wamkulu basi monga izo zinachitira kumbuyo uko. Ndipo iwo anatengedwera kukalowa mu Babeloni. Ndi kulondola uko? Ndipo Baibulo linati, "Mngelo wa Ambuye anaitana ndipo anati, 'Tulukanimo mu Babeloni, anthu Anga!'"

80 Chisokonezo! Izi, "Ndine M'baptisti. Ndine Mmethodisti. Ndine Mpresbateria," zonse izo ndi chisokonezo. Mulibe chipulumutso mwa izo konse.

81 Tsopano, musati muziti ine ndikuti anthu Abaptisti alibe chipulumutso, anthu Amethodisti. Ine sindikuyankhula za izo. Ine ndikuyankhula za mpingo ndi mphamvu yake yandale, ndale zake. Ndi kuyankhula mwandale, chifukwa ndinu Amethodisti, kapena Abaptisti, kapena Mpresbateria, kapena Mkatolika, ziribe kanthu kochita ndi Icho. Mulungu sachizindikira nkomwe icho, ndipo izo ziri mwa Babeloni lero. Ndipo Mulungu ali kuitana Mpingo utuluke kuchokera mwa iyo yonse, kukokera kunja owona mu mtima, kuupanga Mpingo Wake. Kukongola kwake!

82 Ndipo zindikirani, ine ndikhoza kunena chinachake pano chimene chinganjenjeneretse, koma ngati—ngati icho chiri . . . Mvetserani, tsopano. Penyani momwe Babeloni . . . Chimene chinachitika ku . . . mu—mu Babeloni, pamene chikakamizo chinabweretsedwa kwa opembedza moona. Kumbukirani, pang'ono okwanira mdzanja okha, Shadireki, Misheki, ndi Abed-enigo, ndi Daniele, mwa—mwa opembedza moona omwe anapita uko mwa kugwidwa, pamene Mulungu anawaitana iwo kuti—kuti awonetse kwenikweni mangamanga awo, chimene iwo anali. Iwo anakakamizidwira mu kupembedza fano. Ndi kulondola uko? Zamafano! Iwo anakakamizidwira mu kupembedza fano, ndipo iwo ankachita kumagwada pamaso pa fano. Ndipo ngati iwo samachita izo, iwo anali kuzunzidwa.

83 O, chithunzi chake chomwe inu mungakhoze kuchisolola kuchokera mu Danieli, Chivumbulutso, kumangiriza izo limodzi ndi kuonetsa mwa Lemba kuti Mpingo uli nkudza mu mtundu womwewo wa chizunzo Iwo usanati uitanidwe kuti utuluke. Umo ndi momwe Mpingo wa Amitundu unalowetsedweramo, umo ndi momwe Mpingo wa Amitundu uti udzachotsedweremo. Momwe iwo unalowera momwemonso iwo udzapita.

84 Ndipo yang'anani momwe iye analionera fanolo. Ndipo tsopano, kumbukirani, fano . . . Tsopano, ano ndi malo akwathu tsopano. Penyani, ine ndikukhulupirira kuti fano limene Mfumu Nebukadinezara analipanga linali la Daniele, munthu woyera. Ngati inu mungazindikire, Mfumu Nebukadinezara anali atamutcha kale Daniele, anamutcha iye "Beteshazara" (limene linali fano lake), ndipo iye anapanga—anapanga chifanizo, ndipo palibe mmodzi pambuyo pa Daniele anali ataponyedwa mu khola la mikango iyi, ndi zina zotero, ndipo iye anati, "Pasakhale mmodzi ati azitumikira milungu ina iliyonse, ndi zina zotero, koma Mulungu wa Daniele." Icho ndithudi chinali chifano cha munthu woyera, chithunthu chachikulu, ndipo aliyense anali woti azigwadira kwa ichi.

85 Koma Mpingo, Shadireki, ndi Misheki, ndi Abede-nigo . . . Danieli pokhala mtsogoleri, monga Khristu pokhala mtsogoleri wa Mpingo.

86 Ndipo iwo anali oti azigwadira pamaso pa chifano ichi ndi kumachita zopembedza kwa chifano. Zindikirani! Ndipo inu mukuzindikira, mu nthawi zimenezo, Danieli anali chete. Ameni! O, ine ndikuyembekeza inu mukumvetsa ichi. Danieli anali chete. Kuwalola iwo . . . iwo ankayenera kuti apange kusankha kwao kwao.

87 Mu tsiku . . . mu kutha kwa nyengo ya Amitundu, kudzakhala kuli chifano, ndipo aliyense adzayenera kumagwada pamaso pa chifano ichi ndi kumachita mapembedzero. Ngakhale icho chikhale choyera monga kalelo, inu simuli woti muzipembedza chifano (kupembedza-chifanizo).

88 Tsopano, zindikirani. O, mai! Pa mapeto pomwe, Danieli akubwera kachiwiri. Zodabwitsa bwanji! Usiku umenewo lisanati phwando lalikulu la adzakazi ndi ena otero, apo panadza Dzanja likulemba pa khoma, "MENE, MENE TEKEL, UPHARSIN," pa khoma lonselo. Ndipo kutanthauzira, panalibe munthu akanakhoza kukupereka, izo zinalembedwa mu malirime osadziwika. Panalibe munthu akanakhoza kuzitanthauzira Izo.

89 Iwo anapita ndipo anakatenga masikolala awo apamwamba. Iwo anati, "Ife sitikuzidziwa."

90 Iwo anapita ndipo anakatenga ambwebwe awo onse ndi akasidi. "Ife sitikudziwa. Ife sitikudziwa kanthu ka Izo. Ife sitinaonepo konse chinenero choterecho, sitinamvepo konse zotero mu moyo wathu."

91 Koma uko kunali mwamuna! Mulungu anali ndi mwamuna Wake, Danieli analipo uko. Anati, "Pitani mukamutenge iye," anati, "pakuti Mzimu wa Mulungu ukukhala mwa iye."

92 Chotero Danieli anadza pamenepo, anayamba kuwerenga ndi kutanthauzira chinenero chimenecho pa khomapo, ndipo iye anapereka . . . Kodi tanthauzolo linali chiani? Osati, "O,

odalitsika mukhale inu, O, mfumu, khalani moyo mpaka kale." Koma ndi kumukana kwakuwisi, kojintcha, kosabisa kwa iye, anati, "Inu mwayezedwa mu muyezo ndipo mwapezeka operewera."

93 Penyani, ndi njira yomweyo. Monga Chauzimu chija chinabweretsedwa mu ufumu wa Amitundu, chotero Chauzimu chikuuchotsa uwu wa Amitundu. Ufumu unalowetsedwa umo ndi Chauzimu, iwo ukutululutsidwa ndi Chauzimu. Makoma a Yerusalemu adzaponderezedwa, adzakhala . . . iye akada . . . "Amitundu adzawutenga iwo mpaka nyengo ya Amitundu idzakhale itatsirizika." Ndiye Mulungu akutembenukira kwa Ayuda. Ameni! O, mai!

94 O, abwenzi, ine ndikukhumba ife tikadatengera izo mmusi ndithu mwabwino. Sichoncho inu? Kukhala pafupi sabata imodzi pa mutu umodzi uwo, mwaona, chotero ife tikadakhoza kufufuza izo bwinobwino kupyola mu Lemba.

95 Izo, penyani, mvetserani—mvetserani mwatcheru tsopano chimene Iye ananena. "Yerusalemu adzaponderezedwa pansi ndi Amitundu mpaka nthawi ya Amitundu idzakhale itatsirizika." Kutenga kwa—kwa Tito, kenako analowa mkati, anamutenga Yerusalemu. Iye anati, "Tsopano—tsopano, inu munamva za chonyansa chopangitsa chipululutso?"

"Eya."

"Chabwino, apo ndi pamene Amitundu anadzalowamo umo."

"Eya, ife tikumvetsa izo," anatero ophunzira.

"Tsopano, Amitundu akhala ali ndi boma lawo tsopano."

"Zedi."

96 "Yerusalemu anali pansi pa boma la Amitundu apo?" Inde, bwana! Aroma. Iwo akadali nalo boma mu—mu Yerusalemu. Ndipo ilo linayambika kumbuyo uko ndi chonyansa chija chopangitsa chipululutso chimene Daniele anachiyankhula.

97 Tsopano Iye anati, "Nthawi imeneyo yayandikira pafupi, pakuti iwo adzagwetsera pansi kachisi uyu ndi kuimikapo Chisilamu cha Omar, chidzaima pamalo omwewa apa, Achimuhamadi, Amitundu. Ndipo icho chidzaima pamenepo."

98 *Amitundu* kutanthauza "wosakhulupirira." Uwo sunali Mpingo, tsopano. Amenewo anali Amitundu, mwaona, osakhulupirira. Tsopano, ndipo iwo udzaima mpaka nyengo ya Amitundu idzakhale itatsirizika. Ndiye pamene nyengo ya Amitundu iti idzakhale itatsirizika, Karonga wamkulu ndi woti adzaimire anthu (Amene ali Khristu) pa nthawi yotsiriza.

99 "Iye anadza kwa Iye," mu Daniele, "Amene tsitsi Lake linali loyera ngati ubweya," monga ife tinamuwona Iye mu Chivumbulutso 1, "kwa wa nthawi Zamakezana. Ndipo

Chiweruzo chinaikidwa ndipo Mabuku anatsegulidwa. Mabuku" (ochuluka) "anatsegulidwa ndipo munthu aliyense anaweruzidwa kuchokera mu Mabuku, zinthu zolembedwa mkati mmenemo." Onani, Mabuku anatsegulidwa, "Iye anamuona Iye akudza, ndipo zikwi khumi kuchulukitsa zikwi khumi anatumikira kwa Iye." Oyera anadza limodzi ndi Iye. Ndi kulondola uko, mu Daniele? "Ndipo Mabuku anatsegulidwa," ilo ndi Bukhu la moyo wako, "ndipo munthu aliyense anaweruzidwa motero, wochimwa, kuweruzidwa motero. Ndipo Bukhu lina linatsegulidwa, "limene linali Bukhu la Moyo, "ndipo munthu aliyense anaweruzidwa."

100 Tsopano zindikirani, nthawizonse muzikumbukira, muzizitenga izi mu *zitatu*. Ngati inu simutero, inu zedi musokonezeka. Panali magulu atatu a anthu anabadwa pa dziko lapansi; panali magulu atatu pachiyambi; adzakhalapo magulu atatu potsiriza. Chiani . . .

101 Yesu anabwerera ndi zikwi khumi kuchulukitsa ka zikwi khumi, anatumikira kwa Iye. Inu mukukumbukira Iye akunena, "Kodi si chinthu chaching'ono kuti inu mutenge . . . kapena chinthu chosakhala chawamba kuti muzitengera ntchito zanu ndi mavuto anu ku malamulo, pamene simudziwa kuti Oyera adzaweruza dziko lapansi?" Oyera adzaweruza dziko lapansi! Aleluya! Ine ndikaganiza za izo, mai! Kumuona Iye akudza, kutali, ndi osambitsidwa-Magazi, zitatha Zakachikwi, chiombolo ndi owomboledwa a mibadwo yonse ataimirira mu Kukhalapo Kwake. Mkwatibwi wosambitsidwa-Magazi!

102 Osangoti iwo amene ali anthu abwino, iwo ndithudi adzaphonya chiukitsiro choyamba. Baibulo linati, "Ndipo otsalira a akufa sanakhalenso moyo mpaka zaka chikwi zitatha." Nkulondola uko? Awo ndi iwo amene anali ndi maina awo atalembedwa mu Bukhu la Moyo wa Mwanawankhosa koma anaukana ubatizo wa Mzimu Woyera.

103 Osankhidwa okha akupita mu nthawi imeneyo. Osankhidwa okha akutenga z—z—Zakachikwi. O, ndiye, m'bale, ndi anthu a mtundu wanji omwe ife tiyenera kukhala? Ine ndikufuna kuti ndidzakhale moyo kupyola mu Zakachikwi! Tiyeni ife tiike pambali cholemetsa chirichonse ndi tchimo limene limatifooketsa ife mophweka. Ngati munthu anena chinthu china cholakwika kapena achita chinthu china mwanjira *iyi,* mpemphereereni iye ndi kumapitirira kuyenda chitsogolo. Lolani chosankha chimodzi chanu chikhale chitaloza kwa Mulungu. Ngati palibe wina aliyense ati akafikeko, inu mukafikeko! Pakuti pakhala pali osankhidwa amene ati adzakhale moyo kupyola mu M'badwo wa Zakachikwi ndipo adzalowamo ndi kutulukamo ndi Khristu kwa zaka chikwi, ndiyeno iwo adzapita mmwamba ku Ulemerero ndi Iye ndi kudzabwerera kachiwiri. Pamene chiukitsiro cha oipa chidzabweretsedwa, ndiye Zakachikwi zidzayambika . . . Zakachikwi zikadzatha,

ndiye Khristu adzapita mmwamba ndi Mpingo, ndipo pakutha kwa zaka chikwi Iye adzabwerera ndi Mpingo.

104 Khristu akudza nthawi zitatu. Nthawi yoyamba, Iye anabwera *kudzaombola* Mpingo Wake. Kodi ndi kulondola uko? Nthawi yachiwiri, Iye akubwera kuti *adzaulandire* Mpingo Wake. Nthawi yachitatu, Iye akubwera *ndi* Mpingo Wake. Mwaona? Iye anabwera *kudzamuwombola* Iye; Iye akubwera *kudzamukwatula* Iye ndi kutengedwera kutali, mu nthawi ya miliri ndi zina zotero; akubwereranso ku *Zakachikwi*, kukhala moyo kupyola mu Zakachikwi.

105 Ndiyeno Mfumu yaikulu ndi Mfumukazi akubwera pansi kudzachita chiweruzo. Chiweruzo cha pa Mpandowachifumu Woyera chaikidwa ndipo Mabuku atsegulidwa. Ndipo apo pakuima owomboledwawo, Mpingo wobadwa ndi Mzimu Woyera wa Mulungu Wamoyo, utaimirira apo mu kukongola Kwake kuti aweruze. "Mabuku anatsegulidwa, chiweruzo chinaikidwa ndipo munthu aliyense anaweruzidwa motero," uyo anali wochimwa. "Ndipo Bukhu lina linatsegulidwa," osati la Mkwatibwi wa Mzimu Woyera, Iye sadzalandira icho konse pakuti Iye ali mu Mkwatulo.

106 Ngati inu muli odzazidwa ndi Mzimu Woyera mmawa uno, ndipo mphamvu ya Mulungu ikuyenderera mu msempha uliwonse wa thupi lanu, ndi ubwino wanji womwe ukadakuchitirani inu kuti mudzaime mu Chiweruzo? Inu mwaweruzidwa kale, ndipo mwalandiridwa kale, ndipo mwadzazidwa, ndipo kale—mwasinthidwira kale mmalo a Mmwambamwamba ndi Khristu Yesu. Osati kuti inu *mudzakhala* muli, inu muli tsopano, pakali pano osinthidwa!

107 "Iwo amene Iye anawaitana, Iye anawalungamitsa; iwo amene Iye anawalungamitsa, Iye anawapatsa ulemerero." Ndipo munthu woomboledwa aliyense mu dziko mmawa uno, yemwe ali pansi pa Magazi a Yesu Khristu, wodzazidwa ndi Mzimu Woyera, *alinawo* Moyo wosatha ndipo sangakhoze kuonongedwa, ndipo ali kale mu malo Ammwambamwamba ndi Khristu Yesu, ndipo sadzabwera konse mu kuweruzidwa. Waomboledwa kale! Kodi si zodabwitsa izo? Mwaona? Waomboledwa kale, akukhala mu malo Ammwambamwamba tsopano ndi Khristu, ndipo ule-. . . wapatsidwa kale ulemerero, wapatsidwa kale ulemerero!

108 Inu mukuti, "M'bale Bill, kodi Lemba limanena choncho?"

109 Yesu ananena zimenezo, kapena Lemba limanena izo, kapena olemba. Paulo, iye anati, "Iwo amene Iye anawalungamitsa, Iye anawapatsa kale ulemerero. Iwo amene Iye anawadzozeratu, Iye anawakonzeratu; iwo amene Iye anawakonzeratu, Iye anawalungamitsa; iwo amene Iye anawalungamitsa, Iye anawapatsa kale ulemerero." Ndi chiani icho? O, mai! (ndikhululukireni ine) Anawapatsa

kale ulemerero! Ndiye ngati ife tiri odzazidwa ndi Mzimu Woyera, misempha yathu ndi umunthu zasungidwa kale mwa Mulungu, kuli thupi laulemerero likuyembekezera kale, ndipo inu muyenera kuti mupite kwa ilo mwamsanga ili likangoti latha. Iwo amene Iye anawalungamitsa, Iye anawapatsa kale ulemerero!

110 Chimene ine ndinali kunena kanthawi kapitako, mthunzi ndi chenicheni. Ndikukhumba ine ndikadakhala ndi maphunziro okwanira kuti ndichitulutsire chimenechi kunja ndi kuchipanga icho momveka ndi mowoneka kwa inu, koma ine basi sindikukhoza kuzipeza izo. Ine ndikudziwa chimene ine ndiri kuchiyankhula, koma ine sindikukhoza kuchipereka icho momwe ine ndikufunira kutero.

111 [Malo osajambulidwa patepi—Mkonzi.]. . . Nyanja Yofiira ndi zinthu zonse izi iwo akuziika. Zipangizo ziri uko, Ayuda, olemera kwenikweni, ndiye zinthu zomwezo zidzawononga msasa wawo kachiwiri. Eya! Iwo adzabwera uko komwe, mizinda ya mdziko. Russia kubwera uko komwe, nati, "Ife tiyenera basi kuti tikhale nazo zinthu izo. Ndi ureniamu ndi zirizonse kumusi uko, ife tiyenera kuti tipite kuti tikazitenge izo." Ndipo pamene iwo akupita kumusiko, ndiye kudzakakhala nkhondo ya Armagedoni. Apo padzakhala pamene Mulungu ati adzaime monga Iye anachitira mu chigwa kwa ana a Israeli ndi kumenya kachiwiri. Koma izo zidzachitika mpaka nyengo ya Amitundu idzakhale itatsirizika. Ndipo pamene nthawi iyo yatsirizidwa, iye wadulidwapo.

112 [Malo opanda kanthu pa tepi—Mkonzi.] Tsopano mwa kulingalira kwanga kodzichepetsa, munthu wokondedwa amene anafunsa funso ili pano, mwa kulingalira kwanga kodzichepetsa pa izi:

10. Anali ndani zimphona izi mu masiku aja?

113 Tsopano, Josephus apo. . . Indedi, ine ndikudziwa, mpingo wathu, inu muli basi monga ine. Ine—ndine mbuli ya kalasi seveni ndipo ine—ine sindisamala za maphunziro ndi zinthu. Ine ndikuganiza ndi cholepheretsa chachikulu chimene Uthenga unayamba wakhala nacho. Komabe, basi nthawizina, ine ndimalitenga bukhu kapena awiri. Tsopano, kuchita kwanga kuli ndi anthu onga inemwini, ife tangokhala tonse pa mzere womwewo, ife tangokhala anthu wamba chabe. Ndipo ine ndiri woyamikira kwambiri. Baibulo linati, "Anthu wamba ankamumva Iye mokondwera." Apamwamba, ndiye panali gulu lina, koma anthu wamba. . . Anthu oponderezedwa a wamba chabe monga ife tiri, anthu amene amamukonda Mulungu ndipo alibe zochuluka za dziko lino, ali ndi ana awo ndi mabanja, ife timamukonda Mulungu ndipo timakonda kupita ku tchalitchi, kupereka z—zovala za pa thupi lathu chifukwa cha Ufumu Wake, chirichonse monga icho. Ife timamukonda Iye, ife tingachite

chirichonse, ndiwo anthu wamba amene ankamumva Iye. Ndipo zikadali mwanjira yomweyo lero, anthu wamba ankamumva Iye mokondwera.

114 Tsopano, munthu wolemera ali nazo zochuluka kwambiri za dziko lapansi zoti aziziganizira, mwaona. Ndi-ndipo munthu weniweniyo kumusi uko yemwe inu simungakhoze kuchita kanthu limodzi naye, pa ophedwa, iye sangapereke chidwi basi ku Izo. Koma anthu wamba chabe ankamumva Iye mokondwera.

115 Ndipo tsopano mu Josephus, zolemba zake, iye anati... Tsopano, apa pali tanthauzo lake la "ana a Mulungu" awa amene ankatenga ana aakazi a anthu. Iye ananena kuti "Mizimu yakugwa imene inali pa dziko lapansi..."

116 Tsopano, inu mukudziwa m...mu Chivumbulutso, mutu 11...kapena wa 7, ayi ndikukupemphani inu...mutu wa 12 wa Chivumbulutso, mkazi ataimirira mu dzuwa. Chinjoka chofiira chinaika mchira wake kuzunguliza awiri pa atatu a magawo a nyenyezi ndipo anazikokera izo ku dziko lapansi." Ife tikuzindikira kuti Satana, pa chiyambi, anaukhazikitsa ufumu mu maiko akumpoto kuti ukhale wokongola kwambiri kuposa umene—kuposa umene Mikaeli anali, ndipo kunali... ndiye iye analengeza nkhondo Kumwamba. Ndipo iye anakoka magawo awiri pa atatu a zinthu zaungelo palimodzi naye. Ndi kulondola uko?

117 Ndi chifukwa chake ife tiri ochepa okha. Ine ndikutanthauza—mbali...mbali yaing'ono ya anthu mmawa uno, mu dera la Chikhristu, anthu obadwa mwa Mzimu Woyera, chifukwa iwo ali mu g—g—gawo laling'ono. Ndiko kulondola.

118 Ndipo ngati inu mutayang'ana mizimu imene inadza kuchokera ku Genesis ndi kuyamba kuukapo, muone kupembedza kopambana kwenikweni kwa mpingo uko, kwapamwamba koposa. Tayang'anani pa iyo mmbuyo kutaliko mwa Kaini, tayang'anani pa iyo lero. Zikubwera kutsikira mmusi momwe kudzalowa, kusunthirabe mmusi kupyolera mwa Afarisi. Ndipo pali magulu awiri a iwo, Mfarisi ndi Msaduki, mwaona, chikumayendabe chitsogolo kupita, ndipo tayang'anani pa iyo lero mu Chikatolika ndi kusuntha kwakukulu monga uko, malo okongola aakulu.

119 Chabwino, tayang'anani pa Abele ndi mwanawankhosa wamng'ono, muone, wawamba chabe. Tayang'anani pa iwo mu masiku a Yesu. Tayang'anani pa iwo njira yonseyo kutsikira mmusi kupyolera mu Lemba pamene inu mukusunthira nazo izo, muone momwe izo ziriri. Ife tiri kukhala apo pomwe mu tsiku ilo limene Mulungu wawuitana Mpingo Wake njira yonse kudutsa mmusimo. Kachingwe kakang'ono ako, kachingwe kofiira kakang'ono ako kamene kadza mmusi kupyola mu Baibulo, njira yonseyo, ka anthu otsukidwa-Magazi. Zindikirani!

120 Tsopano, "ana a Mulungu" awa, mwa kulingalira kwanga, osati, ndithudi osati kusagwirizana kapena kuyesera kuchita mwanzeru kapena kunena kuti Josephus sanali kudziwa chimene iye anali kuchiyankhula, koma iye anali munthu monga ine ndiri. Ziribe kanthu kuti iye anali sikolala mochuluka chotani, iye anali munthu chabe. Ndipo chinthu chokha chimene iye anali nacho, iye ankafufuza zolembedwa zakale, ndi zina zotero monga choncho, ndi maulaliki akale, ndi zina zotero, koma iye sanali ndi zochulukira kuposa zomwe ife tiri nazo lero, Mzimu Woyera. Tsopano, iye ankangopita mwa lingaliro lachibadwa.

121 Koma ife tikuzitenga izi mwa lingaliro lauzimu. "Ana a Mulungu," aja, pamene . . . kuti iwo anali zinthu zaungelo. Ine ndikukhulupirira iwo ali. Ndipo ine—ine ndikukhulupirira kuti . . .

122 Tsopano, Josephus ananena chinthu chomwecho, koma iye anati, "Iwo anadzikakamiza okha ndi kudzikanikizitsa okha kulowa mu thupi laumunthu, ndipo ankawatenga ana . . . ndi—ndipo ankawatenga ana aakazi a anthu." Tsopano, ndife gulu losakanikira; ndife osiyana pano mmawa uno, amuna, akazi, ndi asungwana aang'ono ndi anyamata, ndipo ine ndikuyankhula izi kuti akuluakulu akhoze ndithudi kuzimvetsa. Koma pamene . . . Iye akunena kuti "Pamene zinthu zaungelo zinaona chikhumbo cha akazi, momwe amuna ankakhalira ndi akazi, kuti iwo ankadzikanikizira okha mu thupi laumunthu. Chotero . . . ndipo iwo ankadzitengera kwa iwo ana aakazi a anthu."

123 Chabwino, ine—ine sindimakhulupirira zimenezo. Ine ndimakhulupirira izi, kuti iwo anabadwira umo mu Kanani, ndipo iwo anabadwa kuchokera mu—mu gulu la Kaini amene anatumizidwa kupita ku dziko la Nodi. Ndipo iye anali ndi chilemba pa iye kuti palibe wina akanati amuphe iye, chifukwa cha chikhalidwe chake chakupha, anamupha m'bale wake. Koma ngati, inu muzindikira, ngakhale Aisraeli anawapeza ena a anthu amenewo pamene iwo ankapita cha kumeneko. Iwo anali aakulu kwambiri, ndipo iye anati, "Ife timaoneka ngati ziwala, pa mbali pa iwo." Ndi kulondola uko? Mazana ndi mazana a zaka mtsogolo, panali anthu aakulu, ojintcha, anthu akuluakulu. Ndipo nthawizina iwo amaikumba—mitembo ya iwo, ndipo iwo amapeza kuti iwo anali anthu aakulu.

124 Tsopano kumene ine ndikuganiza kuti iwo anachokera. Tsopano, pano pali kochepa ka kachiphunzitso kanga komwe tsopano. Ndi anthu a mpingowu basi, mwaona. Ine ndikuganiza kuti Kaini anali mwana wa Satana. Ine ndikudziwa kuti inu simugwirizana ndi izo, mpingo wanga womwe umatero. Koma izo zikanali . . . mpaka Mulungu atandionetsa ine mosiyana, ine—ine ndizikhulupirira chinthu chomwecho, mwaona, kuti iye anali mwana wa Satana. Chifukwa ine sindikadakhoza kuukhazikitsa mzimu wopanda umulungu uwo, wakupha

kubwera kuchokera kwa Mulungu. Ayi, bwana. Iye ankayenera kuti akhale atatengera abambo ake, ndipo abambo ake anali uyu . . . pano, pamene Satana anadza pa serpenti.

125 Ndipo serpenti sanali wokwawa, themberero linampanga iye chokwawa. Iye anali basi monga munthu, iye ankayenda chachiriri. Ndipo iye anali ndi mkazi uyu kunja uko, ndipo iye anachita chigololo ichi ndipo anabala mwana wake woyamba yemwe anali Kaini, wa chikhalidwe cha bambo wake. Ndipo ine ndikukhulupirira chirombo chachikulu icho chinali choimirira ngati munthu, ndipo icho chinkayenda chachiriri, ndipo uko ndi kumene zimphona zazikuluzo zinachokera. Eya, ndizo ndendende. Tsopano, ilo ndi ganizo langa langa ndipo ine—ine ndikhoza kukhala ndi kulakwitsa. Ilo ndi ganizo langa, mwaona. Koma iwo anali anthu aakulu.

126 Ndipo ngati inu mukanazindikira, Mulungu ataima apo pamaso pa Adamu ndi Eva, Iye akuti, "Ine ndinakutenga iwe kuchokera ku fumbi, kufumbi iwe udzabwerera. Ine . . .

127 "Ndipo chifukwa iwe wabweretsa zako . . . iwe unamvetsera kwa wako . . . chirombo mmalo mwa kwa mwamuna wako, kuti iwe unatenga moyo kuuchotsa ku dziko, iwe udzaubwezeranso iwo mu dziko."

128 Ndipo Iye anati, "Serpenti, yachoka miyendo yako, mukuona, iwe suziyenda chachiriri panonso. Ndipo iwe sukhala uli chirombo, iwe ukhala uli chokwawa tsopano. Ndipo pa mimba yako iwe uziyenda, ndipo fumbi lizikhala chakudya chako."

129 Uko ndi kumene ine ndikuganiza kuti iwo . . . Kaini, potengera chikhalidwe cha wakuthengo uyo amene anagona naye . . . monga chinyama, amene anagona ndi mkazi amene anabala mwana uyu, amene anali theka chakuthengo ndi wonga-munthu, munthu wamkulu wachikale. Ndiyeno iye anapita kunja uko ndipo ana ake anayamba kubwerapo kuchokera mwa iye, ndiyeno zirombo, zazilakolako za kugonana monga bambo wao wapachiyambi, chirombo chakale chokhumbira chija chinapeza ana aakazi awa ndi zinthu, ndipo anazitengera kwa iwo ana aakazi anthu. Ndiko kulondola.

130 Ndipo chimene chinabweretsedwa pa anthu awa, zedi chinabwera mmusi kupyolera mu mzere womwewo umene unali mizimu yakugwa iyi imene inadza pa anthu. Kumbukirani, mizimu yomweyo imene inalipo kumbuyo uko, lero . . . ilimoyo lero.

131 Tayang'anani pa iyo lero! Chabwino, ife tiri ndi anthu mu dziko lino amene . . . Tsopano, ine sindiri . . . Ichi, ndine Mmerika, inu mukudziwa ine ndiri. Koma ndiroleni ine ndikuuzeni inu, lino ndi fuko lotsikitsitsa kunja kwa Paris, France, lomwe ine ndikulidziwa mwa kulikonse mu dziko lapansi. Ili ndi lotsika chikhalidwe!

132 Bwanji, ngakhale anthu achilendo, mu Afrika, mu—mu Swedeni ndi . . . kumtunda uko, iwo amati, "Nchiani mu dziko chavuta ndi inu anthu Achimereka, kodi inu nonse mulibiletu ulemu mwa azimayi anu? Mwa nyimbo zonsezi pa wailesi, china chake cha nyimbo zachikale zonyansa, zotukwana zokhudza akazi. Kodi inu mulibe ulemu kwa azimayi anu kumeneko?"

133 Nyimbo zathu zonse ndi zokhudza akazi, kapena kugonana, ndi kukhumbira, ndi zinthu zonga izo. Ndi chifukwa kuti Mdierekezi wagwira pa ilo. Uko nkulondola ndendende. Hollywood yakaleyo ndi matelevizioni ndi chirichonse zikukankhira kunja zinthu zotukwana ndi zopanda umulungu, zidzapita ku malo atsopano ogulitsira ndi china chirichonse. Chirichonse ndi akazi ena ovula kapena chinachake. Ndizo ndendende chimene chinayambitsa izo pachiyambi, ndipo zikuthera mwanjira yomweyo. Ndi zamanyazi!

134 Ndipo msana wa fuko lirilonse ndi ukazi, pamene zifika pa makhalidwe. Ndipo inu mukaphwasula umayi, inu mwaphwasula fuko lanu. Ife tafika pa malo lero mpaka akazi athu . . . akusuta ndudu, ndi zinthu monga choncho, ndi kumamwa kachasu, ndi kumapitiriza motero, ndipo ndi—ndi chamanyazi!

135 Mwamuna wamng'ono kuyesera kuti apeze mkazi amene ali namwali, amene ali wakhalidwe, iye akadayenera kuti apite cha ku mpingo winawake wabwino, waung'ono, wachikale, wa Mzimu Woyera, pafupifupi kuti akamupeze mmodzi; ndipo ndiko kulondola ndendende, kumene amuna amangomusunga iye umo ndi zinthu monga choncho, ndipo ali nako kakhalidwe pang'ono pa iye.

136 Inu mukhoza kuganiza izo ndi zopenga, koma, m'bale, inu muziyang'ane izo mobwereza ndi kukazifufuza, ndipo muone ngati izo siziri Choonadi. Ndi chamanyazi! Chabwino.

Awo anali ana a Mulungu amene ali pa . . . Tsopano, izo, ine ndikhoza kufotokoza zanga . . . Pamene—pamene ine ndikudziwa ngati . . .

137 Ine ndinali ndi funso lina lero, iwo amati, "Bwanji, M'bale Bill, Baibulo linati Eva anati, 'Ine ndalandira mwana kuchokera kwa Ambuye.'" Kulondola ndendende. Iye anayenera kudza kuchokera kwa Ambuye. Ambuye ndi Mlengi yekha yemwe alipo. Iye . . . Mulungu anamulenga Mdierekezi. Ziri motani izo? Mulungu anamulenga Mdierekezi. Mulungu analenga mngelo wakugwa aliyense amene alipo. Ndi kulondola uko? Bwanji, ndithudi. Uko kunali kusankha kwawo, osati Kwake. Iye anakulengani inu, kodi inu mukuchita chiani nazo? Inu mudzaweruzidwa mwanjira yomweyo monga iwo ali. Ndi inu apo. Ndithudi!

138 Awa anali ana a Mulungu, koma iwo anali atagwa ku chisomo ndipo anali atabwera mwa anthu auchirombo awa,

ndipo anathamangira kunja ndi kumakakhumbira. Pamene iwo ankawaona akazi, iwo ankangowatenga iwo. Bwanji, akanalipo kuno. Kupanda makhalidwe kwa Amereka nkodzala ndi... Amuna opanda Mzimu wa Mulungu, angakhoze kuponya khanda atamchotsa mmikono ya amayi ake ndi kumuchita zoipa. Opanda Mulungu, iye si—iye si wabwinoko kwambiri kuposa chirombo. Iye akadali nacho chikhalidwe chauchirombo icho, chopanda umulungu. Ndipo mwamuna ali ndi...Iwo amati, chipembedzo chimakutengera iwe...amati anthu anapenga nacho chipembedzo. Chipembedzo ndi chinthu chokha chimene chingakhoze kumupatsa munthu malingaliro ake oyenera, ndicho, chipembedzo cha Yesu Khristu.

139 Ine ndikhoza kutsimikizira ndi Baibulo kuti inu simuli mu malingaliro anu oyenera mpaka inu mutapeza Khristu. Ndiko kulondola. Izo nzolimba kwambiri, koma ine ndikhoza kutsimikizira izo ndi Lemba. Ndiko kulondola. Inu mumakhala mwauchirombo, kukhumbira, ndi chirichonse, mpaka inu mutapeza Khristu Yesu. Iye ndiye Mmodzi wokondekayo.

140 Tsopano, ine ndivomereza kuti anthu amaphunzira mochuluka kwambiri, ndi kuyesera kupita patali kwambiri mtsogolo, ndi kumayesera kuganiza molimba kwambiri, ndipo nthawizina amakhala ndi kusokonezeka kwa ubongo ndi zinthu pa chifukwa cha kuphunzira za Ambuye. Inu muyenera kuleka izo! Inu simuyenera kuti muzichita izo. Chinthu chokha chimene inu muyenera kumachita ndi kukhala mu chikondi ndi Iye, ndi kumangopitirira nazobe kumukonda Iye. Ameni. Si kuyesera kudzikankhira mu chinachake kapena kudzipanga nokha chinachake chimene simuli, zingopitanibe chitsogolo ndi kulola Mulungu azikugwiritsani ntchito momwe Iye akufunira. Mungodzikhuthula nokha, dziperekeni nokha ndi kumayenda chamtsogolo, mokondwa, mukuimba, mukusangalala. Ndiyo njira yake.

141 Baibulo linati, "Zinthu zonse zimachitira limodzi mwa ubwino wa iwo amene amamukonda Iye," kotero ingokhalani otsimikiza kuti inu mumamukonda Iye, ndicho chinthu chokha chimene inu muyenera kuti muzichidziwa. Ameni! Ingomkondani Iye ndi kumayenda chitsogolo! Zitini, "Ambuye, ine ndimakukondani Inu, Inu mukudziwa ine ndimamukukondani Inu."

"Iwe ukuzikonda *izi*?"

"Ayi, Bwana. Ine ndimakukondani Inu, Ambuye." Mwaona?

142 Kuti, "Chabwino, kodi iwe sukufuna kuti ukhale...Kodi iwe sungakonde kuti ukhale mlaliki wamkulu? Kodi sungakonde kuti ukhale *izi*?"

143 "Ayi. Tsopano, Ambuye, chomwe...Ngati Inu mukufuna kuti ine ndikhale, ine nditero. Ngati Inu simukufuna, Ameni.

Ine ndikhala ndiri pomwe pano, choponderapakhomo pa mpingo uno basi."

144 "Chabwino, tsopano, ine ndikukhulupirira ngati iwe uchita chinachake chonga *izi*, anthu akanamaganiza zochuluka kwambiri za mpingo wanu."

145 "Ine sindikusamala chimene anthu akuganiza, ine ndikufuna kuti ndidziwe chimene Inu mukuganiza, Ambuye. Ine—ine ndingokhala ndi Inu basi, chimene Inu muti mundiuze ine kuti ndichite. Ine ndimawakonda onse awo, zedi."

"Chabwino, tsopano, iwe ukudziwa mlongo *Wakuti-n-wakuti*, iwe sumamukonda iye."

"Inde, ine ndimatero, Ambuye. Inde, ine ndithudi ndimatero. Ine ndimamukonda iye."

"Chifukwa?"

146 "Chifukwa Inu mumamukonda iye, ndipo Inu muli mwa ine. Ndipo ine ndiyenera kumamukonda iye, chifukwa ndi Inu mwa ine mukumukonda iye kupyolera mwa ine." Fyuu! Izo zidzachitenga icho.

147 Koma ine ndikuganiza kuti izo zinali zirombo zija zimene zinagwa mmenemo, ndicho chirombo chokhumbira chimene chidagwa, mwaona.

11. Kodi "ana a Mulungu" akutanthauza Angelo kapena izimu yochokera Kumwamba?

148 Ilo linali funso la munthu. Chabwino. Inu ndikukhulupirira kuti iwo sanali Angelo. Onani, iwo anali okhalapo, "ana a Mulungu," monga Lemba likunenera. Osati angelo, iwo anali ana a Mulungu. Ndipo iwo anabwera kuchokera Kumwamba ku dziko lapansi, ndipo anadzaikidwa mu thupi; osati "anadzikanikizira okha kulowa mthupi," ine ndikukhulupirira kuti mnofu wonse ndi wobadwa mwakugonana kunja kwa Yesu Khristu. Ine ndikukhulupirira kuti Iye ndi munthu yekha anabadwa mwanamwali yemwe anayamba wakhalapo, Yesu Khristu. Ndipo ine—ine sindimagwirizana ndi Josephus pa izo, pa wambiriyakale wamkulu uja. Koma ine ndimakhulupirira kuti iwo anali zokhalapo zauzimu amene anatsika ndipo anadzavala mzimu wa munthu. Ndipo ine ndikukhulupirira kuti iwo ali pomwe pano lero, akuyendabe mozungulira mu Jeffersonville lero, mizimu yauchirombo iyo, yosirira, yopanda umulungu, yomwe ikukhala mu matupi a anthu momwe. Tsopano, tsiku lina anthu awa adzafa; ndipo ngati kuli m'badwo wina, iyo idzadza mmusi momwe kwa iwo.

149 Kumbukirani, Mulungu amamutenga munthu Wake koma osati Mzimu Wake, uwu ndi Mzimu Woyera womwewo umene iwo anaulandira pa Pentekoste.

150 Ndi Mdierekezi yemweyo (mwa maonekedwe achipembedzo) yemwe anamuzunza Khristu, ndi Mdierekezi yemweyo amene ali

mu mpingo lero, akuvala miinjiro yaitali. Ndipo iwo sakusowa kuti azichita kumavala . . . Ine sindikutanthauza mwinjiro wa pa thupi lawo, ine ndikutanthauza mwinjiro wa pa solo yanu. Mwaona, "Pakuti, masiku a zozizwa anapita, palibe chinthu chonga izo ayi." Inu mukanena za Afarisi amakono! Ndendende basi.

151 "Okhala nawo . . . " Baibulo limati, "Iwo adzakhala nawo maonekedwe aumulungu, koma azidzakana Mphamvu yake. Kwa oterowo dzipatuleni, chokani kwa izo. Ingokhala kutali, dzisungeni nokha kutali." Iwo akanali ana a Mulungu aja, koma ali mu chikhalidwe chakugwa. Mukuona chomwe ine ndikutanthauza? Ena a iwo ndi atumiki, ena a iwo ndi madikoni, ena a iwo ndi akulu, ena a iwo ndi mabishopu, ongokhala achipembedzo momwe iwo angathere kukhala! Koma Baibulo . . .

152 Tsopano, ine ndiliyankha funso, m'bale, limene inu munandifunsa ine kanthawi kapitako. Winawake anati:

12. M'bale Branham, ine ndikufuna kuti ndidziwe malo amene ine ndingakhoze kumangirirapo ndi kuti, "Munthu uyu ali nawo Mzimu Woyera chifukwa iye anachita 'izi,'" kapena "Mkazi uyu ali nawo Mzimu Woyera chifukwa iye anachita "izo."'"

153 Palibiretu njira mu dziko kwa inu kuti mudziwire izo. Ndiko kulondola. Palibe njira mu dziko loti inu mudziwire izo. Mulungu ndiye woweruza, ife sitiyenera kuti tiziweruza. Mwaona? Zingolalikirani Uthenga, zikhalani moyo . . .

154 Munthu anadza kwa ine kuno nthawi ina kalelo, ine ndinali ndikulalikira za chimene ine ndinanena usiku wina. Iye anabwera ku nyumba yanga ndipo iye anati, "M'bale Branham, m'bale, ine ndikufuna—ine ndikufuna—ine ndimafuna kuti ndikhale . . . Ine ndikufuna kuti ndiwachotse machimo anga. Ine ndikufuna kuti ndikhale Mkhristu." Iye anakhala pa khonde langa.

155 Iye anati, "Ine ndinamvapo za mwamuna wamkulu, mwamuna wodziwika konsekonse dzina lake Billy Graham." Iye anati, "Ine ndinapita ku misonkhano yake ndi—ndi—ndipo iye anati, 'Onse amene akufuna kuti akhale Akhristu, kwezani mmwamba dzanja lanu ndipo mumulandire Khristu ngati Mpulumutsi wanu wanu.' Kotero ine ndinakweza mmwamba dzanja langa. Iye anati, 'Tsopano, nonse imiririrani, ife tikhala ndi pemphero.' Kotero ine ndinakhala ndikupemphera basi . . . " (mundikhululukire ine) "modzipereka basi monga ine ndikanathera." Iye anati, "Ndipo, koma izo sizinandichitire ine ubwino uliwonse."

156 Iye anati, "Ndiye ine ndinapita uko ku—ku msonkhano wa Oral Roberts." Iye anati, "Ine ndinamva za iye, ndipo ine ndinamva kuti iwo onse anali ndi chimwemwe chotero." Anati,

"Ine ndinapita uko kwa Oral Roberts ndipo ine ndinakamufunsa iye, 'Kodi ine ndiyenera kuchita chiani kuti ndikhale Mkhristu?' Iye anati, 'Iwe ubwerere mkati umo . . .' Ine ndinamuuza iye ine ndinakwezapo mmwamba dzanja langa kwa Billy Graham. Iye anati, 'Iwe ukakhale mu chipinda chofunsira icho mkati mmenemo mpaka iwe ukhale wosangalala kwambiri mpaka uyankhule mu malirime.'" Iye anati, "Ine ndinapita mmenemo ndipo ine ndinapemphera mpaka ine ndinayankhula ndi malirime." Anati, "Ine ndinabwerapo, sichinandichitire ine ubwino uliwonse."

157 Iye anati, "Ndiyeno ine ndinapita ku msonkhano wina ndipo iwo anandiuza ine ndinali ndisanayeretsedwe apobe, anati ine 'Ndiyenera kuti ndiyeretsedwe ndi kukhala wosangalala ndi kumafuula, kupeza chimwemwe chokwanira.' Kotero ine ndinapemphera ndi kupemphera mpaka ine—ine ndinafuula." Iye anati, "Apobe . . . "

158 Ine ndinati, "M'bale, chirichonse cha zinthu izo ndi cholondola, chirichonse cha izo ndi chabwino. Kuimika mmwamba dzanja lako, kuyankhula ndi malirime, kufuula, ine ndimakhulupirira mu kanusu kalikonse ka izo, komabe si ndicho chinthucho. Mwaona, ndi kumulandira Munthuyo, Khristu Yesu." Mwaona? Mwaona, si ndicho . . .

159 Zinthu izi ndi zotsatira. Kufuula, kuyankhula mu malirime, kuthamanga, kufuula, kumalira, kupemphera, chirichonse, izo ndi zotsatira chabe zimene zimatsatirapo. Chinthu choyambirira ndi kumulandira Munthuyo, Khristu Yesu. Mwaona? Kotero palibe ayi—palibiletu umboni umene ife tingakhoze kunena. Chifukwa munthu amalira? Ine ndamuwonapo munthu akulira ndi kulira, ndi kumalira misozi ya ng'ona, ndipo iye akadali wochimwa wamkulu momwe iye akadakhoza kukhala ali.

160 Mvetserani, Yesu amatifanizitsa ife ndi nkhosa. Ndi kulondola uko? M'busa amazidziwa nkhosa zake. Alipo muno anayamba waimva mbuzi ikulira? Chabwino, m'bale, inu kulibwino mukhale muli m'busa ngati inu mukufuna kuti mudziwe kusiyana kwake. Mbuzi imalira mofanana basi monga nkhosa. U-nhu. Siyani kambuzi kakang'ono ako kakoledwe uko penapake, ndi kankhosa kakang'ono pa mbali inayo, "Bee," ndiyeno "Bee," mofanana basi.

161 Ndipo ine ndawamvapo iwo pansi pa guwa akungolira ndi kumalira, O, Mulungu!" kumangosisima motero monga choncho, "O, Mulungu!" ndipo ali mbuzi nthawi yonseyo. Ndiko kulondola. Kufuula? Chabwino, mai, ine ndawaona iwo akufuula mpaka iwo basi . . . ndipo iwo amathamanga kudutsa ponsepo ndi kumalumpha mmwamba-ndi-pansi ndi kumafuula.

162 Tsopano, inu mukuti, "M'bale Branham, inu simumakhulupirira za kulira!"

163 Musati muzinditenga ine molakwitsa. Zedi, ine ndimakhulupirira za kulira. Koma ine ndikunena kuti uwo si umboni ayi, mwaona, chifukwa onsewo amalira. Ine ndawaona onse akufuula molimba basi monga iwo akadathera kufuula. Inde, bwana. Ndi basi kumangopitirizabe monga choncho, ndipo pali mitunda yaitali, inu mukudziwa zomwe ine ndikuziyankhula. Ine ndawamva iwo akuyankhula ndi malirime, kupita kunja ndi kumakakhala moyo wa mtundu uliwonse, kumangochita chirichonse. Icho sichinali chizindikiro.

Koma inu mukuti, "Inu mukutsutsana nazo."

164 Ayi, ine sindiri. Ine ndimakhulupirira za kuyankhula mu malirime, ndi mphatso ya Mulungu mu mpingo. Ngati ine ndikanazichotsa izo, ine ndikanachotsa gawo la Mulungu. Ngati ine ndingachotse lirime langa—lirime langa kulichotsa pa thupi langa pano, ine sindikanakhala ndi thupi lathunthu. Thupi la Yesu Khristu liri ndi malirime mu Ilo. Thupi la Yesu Khristu pano liri ndi malirime; ndipo inu mukalichotsamo ilo, inu muchotsa gawo la Khristu. Koma inu simungakhoze kunenabe kuti ilo ndilo Thupilo, mwaona. Mwaona? Mwaona?

165 Koma ndi kulandira Munthuyo, Khristu Yesu, ndipo zinthu zina izi zimadza kumene mkatimo ndipo izo zimagwirizana limodzi. Muloleni membala aliyense mu thupi lino mmawa uno, kaloleni kagulu kakang'ono aka ka anthu, ngati ife tikadakhoza kukokera makatani pansi apo ku mbali iliyonse ndipo munthu aliyense mkati muno nkumulandira Munthuyo, Khristu Yesu, si pakadakhala mkangano nkomwe kapena sipangakhale nkomwe mtsutsano. Pakadangokhala chikondi changwiro. Komabe inu mukadamakhulupirira *izi* ndi kumakhulupirira *izo*, koma izo zikadangokhala zodzaza ndi chikondi inu mukadangoti... Mwaona? Ndi zimenezo. Tsopano, Yesu anati, "Ndi chipatso chawo inu mudzawadziwa iwo." Ndipo chipatso cha Mzimu ndi chikondi, chimwemwe, mtendere, kupirira motalika, ubwino, kudzichepetsa, kufatsa.

166 Tsopano, ine ndati...Ine ndikupatsani inu kuyesa kwanga kwa chimene ine ndikuganiza kuti ndicho chinthu chapafupifupi kwa umboni, woti munthuyo ndi Mkhristu, koposa chinachirichonse chimene ine ndikuchidziwa. Kodi inu mukudziwa chomwe icho chiri? Ndiko kuvutika kwa mmoyo. Munthu yemwe nthawizonse akumva njala kwambiri ndi kumva ludzu lofuna Mulungu. Iwo basi mophweka...usana ndi usiku, iwo—iwo sangakhoze basi kupirira nazo. Iwo—iwo—iwo ayenera kuti amchitire Mulungu chinachake. Iwo—iwo ndi odzala ndi chikondi ndipo iwo ali basi...kuusa-moyo, kumangovutika mmoyo nthawi zonse. Baibulo linati, "Iye amene apita akufesa mu misozi mosakaika adzabwererako, akusangalala, akubweretsa pamodzi naye mitolo yofunika." Ndi kulondola uko? Zinthu zonse izo.

167 Tsopano, penyani, ngati apo. . . Ngati mpingo uwu. . . Ngati ine ndikadanena, mmawa uno, kuti gulu ili pano la anthu ndi ine. . . Ndipo Mulungu nkuti, "Tsopano, taona William Branham, ine ndikupanga iwe kuti udzayankhire kwa gulu ilo la anthu, chimene iwe ukuwauza iwo. Tsopano, kodi iwe ukufuna iwo onse kuti azifuula?"

"Zedi, ine ndikufuna iwo kuti azifuula."

"Kodi iwe ukufuna iwo onse kuti aziyankhula ndi malirime?"

"Ine ndikufuna aliyense wa iwo azitero."

"Kodi iwe ukufuna iwo onse kuti azivina mu Mzimu?"

"Ine ndikufuna aliyense wa iwo azitero."

168 "Zonse ziri bwino, chabwino, izo nzabwino kwambiri, koma nchiani iwe ukadakondetsetsa maka kuti iwo anayenera kumachita?" U-nhu

169 "Ine ndikanafuna maka kukhala ndi mpingo umene unali ndi kulemedwa kotero pa mtima wawo pofuna pemphero kuti iwo akanangomakhala pa guwa ili ndipo akadamakhala ali pano usana ndi usiku, ndi china chirichonse; ndi mu manyumba awo, ali mosalekeza mu pemphero, ndi kudzichepetsa, ndi kumayesera kumawatenga anthu kuti abwere kwa Mulungu, ndi kumakayendera anthu ku chipatala ndi kumachezera odwala, ndi kumayesera kuti aziwatengera anthu kuti abwere ku mpingo ndi kumachita molondola. Ine ndikanafuna kukhala ndi izo kuposa zina zonsezo kuziika pamodzi; ngakhale zinazo ndi zabwino, izo ndi za mu mpingo."

170 Koma ngati ine ndikanati ndikhale ndi izo, ine ndikanaziyika izo poyambirira. Chifukwa ngati iwe uli nazo izo, zinazo zidzachitika. U-nhu. Mwaona? Ngati iwe uli nazo izo, ngati inu mudzangokhala anjala kwambiri ya kwa Mulungu, kufuula kudzayamba kuchitika. Ngati inu mudzakhala anjala kwambiri ya kwa Mulungu, kuyankhula mu malirime kudzachitika. Ngati inu mukhala ndi njala yambiri ya kwa Mulungu, ndipo inu mupitirirabe kumamva njala, kudzisunga izi. Mudziona nokha mukukhala osiyana, ingokumbukirani, yang'anirani, pali mzimu wina ukuyesera kuti udzichititsire wokha mmenemo. Mukhale mwaubwino pamaso pa Mulungu, odzichepetsa, ndi kuusa kwa moyo. Mungokhala. . . uchikale wanu wonse wabwino. . .

171 Ine ndikhoza kutsimikizira ndi Baibulo kuti "Nthawi yoyamba Mngelo wa Mulungu anapita pamwamba pa dziko kuti akasindikize ndi Mzimu Woyera, Iye anangowasindikiza iwo amene ankalira ndi kuusa moyo chifukwa cha matemberero omwe ankachitidwa mu mzinda," Ezekieli, mutu wa 9. Nkulondola uko? Anaika chizindikiro pa mphumi pa iwo

amene ankausamoyo ndi kulira chifukwa cha zonyansa zomwe zinkachitidwa mu mzinda.

172 Tsopano, ine ndikufuna kuti ndikufunseni inu funso, ine ndikufunsani inu funso ili. (Tsopano ife titseka mwamsanga ndithu momwe ine ndingathere.) Chikadachitika ndi chiani lero ngati Mzimu Woyera ukanapita ukudutsa mu Jeffersonville, New Albany, ndi Louisville, kuti adzawasindikize iwo masana ano amene akadakhala ali ku nyumba, "Mulungu, tumizani chitsitsimutso, kungokhala anjala kwambiri kufuna msonkhano. O Mulungu, tayang'anani pa machimo a mzindawu. O, kodi izo si zoopsya, Mulungu? O, kodi Inu chonde simutumiza chitsitsimutso, Mulungu. Tumizani mlaliki wina wabwino, tumizani wina. O Ambuye, mulole Mzimu Woyera basi . . . " Nkuti, nkuti kumene Iye akadakasindikiza? Ganizani za izo.

173 Tsopano, "Chabwino, M'bale Branham, inu mukutanthauza chiani?"

174 Ine ndikutanthauza izi, ndipo ine ndikunena izi tsopano mwaulemu, ndikuyenda pa ulusi wosachedwa kuduka. Ine ndikhulupirira tsiku limenelo liri pafupi kutha, iwo amene ali mkati ali mkati. Mukuona? Mukuona? Zitseko zikutsekedwa palimodzi, inu mulibe kulemedwa kumeneko panonso.

175 Billy Graham anali ndi misonkhano monse kudutsa dziko, ndi Oral Roberts, ndi tonse a ife. Ife talira, ndipo tapemphera ndi kupemphera, ndi china chirichonse. Koma, inu mukuona, zitseko zikutsekeka. "Msiyeni iye amene ali woyipa," ine ndikubwereza Lemba, "akhale chiyipirebe. Msiyeni iye amene ali wolungama, akhale chilungamirebe. Iye amene ali woyera, akhale chiyererebe." Ndipo ine ndikukhulupirira kuti zitseko za Amitundu zikutsekeka palimodzi. Mwaona? Tsiku la nthawi ya nyengo liri pafupi kutha kwenikweni, ochulukira mochepa chabe kuti adze mkati. Chifukwa chimene inu simukukhoza kukhala ndi msonkhano wa mtundu uliwonse wonga iwo, palibe kuusa kwa moyo. Inu mulibe—inu simukukhala nako kulemedwa kumeneko.

176 Ine ndikukumbukira zaka zapitazo. Inu nthawizonse mumawamva iwo akuyankhula za tinjira ta utuchi ndi zinthu mu Kachisi. Izo sizinapangitse icho kuchulukira kulikonse, osati pang'ono mochulukira. Koma ndiye icho chinali chatsopano, Mulungu anali akuwuitana Mpingo Wake. Ine ndawaonapo iwo akuusamoyo ndi kulira ndi kukhala pa guwa utali wa usiku wonse. Ine ndapitapo ku manyumba awo, ndipo iwe umakhoza kumawamva iwo pamene iwe ukubwera, basi mu zao . . . mu zipinda zao zogona, amuna ndi akazi, akulira, "O Mulungu!"

177 Inu mumakhoza kuwaona iwo akuyenda kudutsa mu mpingo, ndipo ine ndimakhoza kuliwona limba likuyamba kuimba, *"Yesu Mundisunge Ine Pafupi ndi Mtanda,"* ndipo misozi kuyenderera ikutsika apo, inu mukudziwa. [M'bale

Branham akufwenthera—Mkonzi.] Akulowa mu mpingo *uwu*, kenako nkuyenda kupita ku mpingo wina, ndi kuwamva iwo uko, *Pali Kasupe wofunika*." "O Mulungu, mpulumutseni mnyamata wanga. Mpulumutseni msungwana wanga, iye wataika, Ambuye. Chonde!"

178 Inu simumazipeza izo panonso. Chavuta ndi chiani? Mzimu wa Mulungu wachotsedwapo. Yesu anati, ananeneratu ichi, kuti chikondi . . . chifukwa chikondi cha ambiri . . . chikondi chao chikadadzalephera. "Kuti chifukwa kusayeruzika kukanati kudzachuluke, chikondi cha ambiri chikanadzalephera." Mwaona? Mwaona, kuzilala, kuchokapo. Chikondi chikuchoka nichifa. Ndipo iwo alowa mu chiani? Maonekedwe chabe; kuomba limba mokweza ndi mositsa, molimbika kwenikweni, ndi kumafuula, "Ulemerero kwa Mulungu! Aleluya! Ameni! Ambuye alemekezeke!" Mwaona, monga choncho, iwo ndi maonekedwe chabe. Musati muzidzipusitsa nokha, mwaona, basi mukungodzipusitsa nokha. Mwaona, vetserani, m'bale, mpaka ife? . . . ine ndizipita monga chonchi, ine ndikuyankhula . . .

179 Ine sindikuyankhula za Kachisi wathuyu, ine ndikuyankhula zomwe ine ndimazipeza kuzungulira United States. Izo zangokhala mwamaonekedwe chabe, kungokhala mwa kuchita kumene ife tinali nako. Ndipo kuusa kwa moyo uko, kwangotsala pafupi kutha. O m'bale, mlongo (Mulungu, achite chifundo pa ife) Mulungu akhale ndi chifundo!

180 Tayang'anani pa zitsitsimutso izi ndi zinthu zikungosinja ndi kusinja ndi kusinja, ndipo Uthenga ukulalikidwa momveka kwambiri, iwo . . . Tayang'anani pa izo lero, basi mwamsanga pamene chitsitsimutso chikutsekedwa, iwo amapita. Inu mukudziwa chiani?

181 Ndiroleni ine ndinene ichi. Ine sindikudziwa chifukwa chimene ine sindikutha kuchoka kwa ichi. Koma, penyani, Yesu anati, "Ufumu wa Kumwamba uli wofanizidwa ndi munthu yemwe anatenga khoka ndipo analiponya ilo mu nyanja. Ndipo pamene iye anagwira umo, iye anakolamo mitundu yambiri ya za mnyanja, ndithu. Iye anakolamo akamba, ndipo anakolamo njoka, ndipo anakolamo nsomba zokwawa, tizirombo ta mmadzi, nsomba. Mwaona? Ndipo ine ndikukhulupiria khokalo . . .

182 Tsopano, penyani! *Apa* pali kamba, ndipo *apa* pali nsomba. Kamba uyo sangakhoze kuchitira mwina chifukwa iye ndi kamba, iye anali kamba pa kuyamba pomwe. Chikhalidwe chake ndi kamba ndipo izo ndi zomwe zinalipo kwa iye. (Tsopano kumbukirani, ine—ine ndinati ine ndimati ndipemphere.) Mwaona, iye ndi kamba pa kuyamba pomwe, iye ndi kamba tsopano. Ngati iyo ili njoka pa kuyamba pomwe, iyo ndi njoka

tsopano. Ngati iye ali kachirombo ka mmadzi pa kuyamba pomwe. . .

183 Ine ndikukhulupirira kuti khokalo laponyedwa ndi kuponyedwa ponyedwa, mpaka pafupifupi nsomba zonse zachotsedwamo mu dziwe.

184 Ndicho chifukwa iwo amati, "Chabwino, ine ndinali nditakweza manja anga. Ulemerero kwa Mulungu! Ine ndikufuna kuti ndipulumutsidwe. Ambuye alemekezeke!" Ndipo masiku angapo kenako, "O, Lydia, iwe ukudziwa zinthu zija ndi nzamkhutu." "Ine ndikulingalira izo zinali kulondola." Chifukwa? Chikhalidwe chiri *umu* ndi kachirombo ka mmadzi pa kuyamba pomwe; anali serpenti, poyamba.

185 Nsomba ziri pafupi kusesedweratu mu nyanjayo tsopano. Khoka likhala litayanikidwa. Ndipo Yesu adzabwera, Iye adzatengera nsomba Zake mkati ndiye. Mukuona chimene ine ndikutanthauza? O, ngati pali kachidutswa kamodzi ka Chikhristu mwa inu, ngati pali kachidutswa kamodzi ka chikhumbo kuti inu muzimutumikira Mulungu, mukagwiritse iko molimba basi monga inu mungathere mmawa uno ndi kukasamalira iko ndi mtima wanu wonse.

186 "Ana a Mulungu anadzitengera kwa iwo ana aakazi a anthu." Zedi iwo anali ana a Mulungu. Lero iwo akadali ana a Mulungu, koma iwo ndi ana okugwa a Mulungu. Ena a iwo, mwamalemba, fyuu! Momwe iwo amathera kuyankhula Lemba! Iwo ndi ana a Mulungu. Inu mukudziwa, Satana anali munthu wakudzanja lamanja la Mulungu. Inu mukudziwa, iye amadziwa zochuluka za Lemba kuposa aliyense—wazamulungu aliyense—wazamulungu mu dziko lero. Kukamba za. . .Iye akuwatembenuza maseminare chadodolido, makamaka imodzi iyi ya Baptisti kumtunda kuno ikunena kuti—kuti "Yesu Khristu anabadwa kuchokera kwa Mroma, kapena msirikali wa chi Germany." Ine ndiri nalo bukhu pa izo, ine ndikufuna ndidzakuonetseni inu ilo ena a masiku awa. Chabwino.

187 Mwamsanga, Eksodo. . .O, ife sitikadakhoza konse kulitenga ilo kupatula ife titaziika mmbuyo. Ine ndiwatenga iwo mwamsanga ndithu tsopano, ine ndikudziwa ine ndikutenga nthawi yanu yambiri. Inu nonse mupilira nane ine utali wa maminiti pang'ono? [Osonkhana ati, "Ameni!"—Mkonzi.]

13. Kodi wani handiredi forte foro sauzande, akutchulidwa mu Chivumbulutso, otsalira a Ayuda omwe ife. . . adzakhala gawo la Mkwatulo wa Mpingo? (utatha) Kodi si Israeli, wa koyamba kwa i. . .iwo anayamba. . .(ine ndikupepesa). . . **akupita mu nthawi—nthawi ya. . .**

188 Ine ndikupepesa, miniti yokha mpaka ine ndifike pozimvetsa izi bwino. Izi—izo zadutsa, izo zabwerezedwera pa pepala.

. . .kuti zifike pochitika zaka chikwi chimodzi cha—cha Khristu kani kuposera momwe munthu angathe kukhalira,

monga amachitira anthu achipembedzo amakono awa amatiuzira ife. Inde, bwana.

189 Tsopano, miniti yokha, kuti ndizitenge izi molondola. Funsolo liri:

Kodi wani handiredi ndi forte-foro sauzande, ndiwo omwe ife tiri otsalira a . . .

190 Ine ndikufuna ife tidzikonze pa chimodzi icho poyamba, basi kuti tikhale otsimikiza kuti inu . . . Mwaona, wani handiredi ndi forte-foro sauzande . . .

Kodi wani handiredi ndi forte-foro sauzande, kutchulidwa mu Chivumbulutso awa, ndiwo otsalira a Chiyuda monga kuti awo adzakhale gawo la Mkwatulo wa Mpingo? Wani handiredi ndi forte-foro sauzande . . .

191 Tsopano, basi . . . Ine ndiri—ine ndiri . . . ine ndikufuna ndimvetse izi momveka mu malingaliro anga ine ndisanayambe pa izo.

Kodi wani handiredi ndi forte-foro sauzande, akutchulidwa mu Chivumbulutso, ndiwo otsalira a Chiyuda omwe ati adzakhale gawo la Mkwatulo wa Mpingo?

192 Ine ndikufuna kuti nditenge izo poyamba. Wani handiredi ndi forte-foro sauzande ndi otsalira a Chiyuda, koma osati Mpingo wokwatulidwa. Mwaona? Yang'anani uko tsopano mu Chivumbulutso, mutu wa 6, inu muziona izo.

193 Ndiye ife titenga gawo linalo pa ina—pa mbali inayo ndipo iwo ali ndi funso lina mmenemo. Zindikirani zinthu izi.

194 Chabwino, penyani apa tsopano, Chivumbulutso 6, tsopano, ndi pamene inu mukuzipeza izo. Mwaona? Tsopano, ife tikuti tiyambire, iye akupitirira ndi kuyankhula za okwera pa kavalo, ndi zina zotero, kupita nazo. "Pamene iwo anatsegula . . . " Tiyeni tipeze ndime ya 9 ya mutu wa 6 wa Chivumbulutso:

Ndipo pamene iye anatsegula chisindikizo cha chisanu, . . .

195 Ine ndi—ine—ine ndalakwitsa, ine ndiri mu mutu wolakwika. Ndi mutu wa 7:

. . . zitatha zinthu izi ine ndinaona angelo anai ataima pa ngodya zinai za dziko lapansi, . . .

196 O, ndi funso lokongola bwanji, ndi nthawi yake yochepa kuti tilowe mu ilo ndi kukhala ndi pemphero pa odwala.

. . . zitachitika zinthu izi ine ndinaona angelo anai akuimirira pa ngodya zinai za dziko lapansi, atagwirizira mphepo zinai za dziko lapansi, kuti mphepo isati iwombe pa *dziko lapansi, kapena pa nyanja, kapena pa mtengo uliwonse.*

> *Ndipo ine ndinaona mngelo wina* akutsika *kuchokera* kumwamba, *ali nacho chisindikizo cha Mulungu wamoyo:. . .*

197 O, khalani otsimikiza, ili ndi funso lodabwitsa. Mwaona? Tsopano, tapenyani chithunzi chasewero; Yohane ananena tsopano, pano. . . kutali ndi dziko lapansi tsopano, mu Mzimu, akuyang'ana mmbuyo ku dziko lapansi. Ndipo iye anaona angelo anai ataima pa ngodya zinai za dziko lapansi, atagwira mphepo zinai za dziko lapansi.

198 Tsopano, "mphepo," mu Baibulo. . . Ine ndiribe nthawi yoti ndikuyendetsereni inu Malemba. Koma ife tikhoza kungofika ku ili. Ngati ilo siliyankhidwa mokhoza, ndiye ine ndidzalitenganso ilo nthawi inayake. Zinai. . . *Mphepo*, mu Baibulo, zimatanthauza "nkhondo ndi makangano." Monga mu nthawi ya Yobu, inu mukukumbukira, mphepo zinatsika pansi ndi—ndipo zinatenga ana. Ndipo inu mukudziwa zomwe ine ndikutanthauza, ichi—ndi—ndi mavuto. Mwaona?

> . . . ndipo *ine ndinaona angelo anai* (*angelo anai,* kapena "atumiki anai"), iwo anali *ataimirira pa* malire a. . . kapena *ngodya zinai za dziko lapansi, atagwira mphepo zinai*. . .
>
> *. . . ndipo iye anafuula ndi liwu lofuula kwa angelo anai, kwa omwe zinapatsidwa kuti—kuti aipse dziko lapansi ndi nyanja.* (Tsopano, ndiko kudza kwa Ambuye, chimene iye akuchiyankhula. Mwaona?
>
> *Akunena, Musaipse dziko lapansi, ngakhale nyanja, kapena mitengo, mpaka ife titasindikiza antchito a Mulungu wathu mu mphumi zao*. (antchito)

199 Tsopano, kumbukirani, Mpingo si antchito Ake. Ife ndife ana Ake, osati antchito Ake. Myuda nthawizonse ndi wantchito Wake. Mpingo sunayambe wakhala antchito Ake, Iwo wakhala uli ana Ake. Mukuona? Antchito:

> *Ndipo ine ndinamva chiwerengero cha iwo. . . anasindikizidwa: ndipo pamenepo anasindikizidwa handiredi ndi forte ndi foro sauzande* onse *a mafuko a ana a Israeli.* (Tsopano, penyani, onse ndi Ayuda)

200 Tsopano penyani! "A fuko la Yuda anasindikizidwa thwelofu sauzande. Fuko la Rubeni, thwelofu. Fuko la Gadi, thwelofu. Aseri, thwelofu. Ndi la Nefitali, thwelofu, ndi—ndi kupitirira mmusi. Simeoni, thwelofu. Ndi Aseri, thwelofu. Ndi Zebuloni, thwelofu. Ndi Benjamini, thwelofu." Ndipo mafuko khumi ndi awiri a Israeli, chotero thwelofu kuchulukitsa ka thwelofu3ndi chiani? Handiredi ndi forte-foro sauzande. Tsopano, penyani, onse a mafuko a ana a Israeli. Tsopano penyani, iwo anali "antchito" a Mulungu.

201 Tsopano mwina ine ndikhoza kuzipanga izi kumveka. Tsopano penyani:

> *Zitatha izi*. . . onani, *ndipo, taonani,* ndipo ine ndinaona *gulu lalikulu, limene palibe munthu akadakhoza kuliwerenga,* (tsopano, pano pali gulu lina, mwaona) *a mafuko onse,* . . . *mitundu,* . . . malirime, *ndi* anthu, ataimirira *pamaso pa mpandowachifumu, ndi pamaso pa Mwanawankhosa,* ali ndi zoyera . . . ali ndi . . . *Mwanawankhosa, atavala miinjiro yoyera, ndi makhwatha mmanja awo;*
>
> *Ndipo* iwo *anafuula ndi liwu lalikulu, kumati,* . . . (Mvetserani kwa msonkhano wa Mzimu Woyera uwu!) . . . *Chipulumutso kwa Mulungu wathu amene akukhala pa mpandowachifumu,* ndi *kwa Mwanawankhosa.*
>
> *Ndipo angelo onse* . . . kuzungulira *mozinga—mozinga mpandowachifumu, ndi mozinga akuluakulu ndi zamoyo zinai,* . . . *zinagwa pamaso pa mpandowachifumu pa nkhope zawo, ndipo anampembedza Mulungu,*
>
> *Kumati, Ameni: Madalitso,* . . . *ulemerero,* . . . *nzeru,* . . . *mayamiko,* . . . *ulemu,* . . . *mphamvu,* . . . *ukulu, zikhale kwa Mulungu wathu kwa nthawi za nthawi. Ameni.*
>
> *Ndipo mmodzi wa aakulu* . . . (Tsopano, penyani tsopano, uyo anali . . . Yohane anali mu masomphenya) . . . *mmodzi wa akulu* anati . . . anandiyankha ine, anati *kwa ine, Kodi awa ndi ayani* . . . (Tsopano, Yohane anali Myuda ndipo iye anawawona mafuko khumi ndi awiri a Israeli, iye ankawadziwa iwo) . . . Koma *awa ndi ayani amene avala miinjiro yoyera? ndipo akuchokera kuti iwo?* Kodi iwo achokera kuti? Tsopano, iwe wawaona Ayuda awo, iwe ukuwadziwa iwo mmodzi aliyense, iwe unawawerenga iwo kuchokera mu mafuko ndi kutchula zikwi zomwe zinasindikizidwa. Koma awa ndi ndani a mtundu uliwonse, lirime, ndi fuko? Kodi iwo anachokera kuti?
>
> *Ndipo ine ndinati kwa iye, Bwana, inu mukudziwa.* (Yohane, mwakuyankhula kwina, "Ine sindikudziwa komwe iwo akuchokera. Ine ndine Myuda ndipo ine ndaima pano, ndipo ine ndikuwaona anga—anthu anga ndi kuwaona awo amene ali pano.") . . . *Ndipo iye anati* kwa *ine, Awa ndi iwo amene abwera kuchokera mu chisautso chachikulu,* . . . (Mwaona?) . . . *chisautso chachikulu, ndipo atsuka miinjiro yawo, ndipo ayipangitsa iyo kuyera mu mwazi* (osati mu umembala

wa mpingo)...koma *mu magazi a Mwanawankhosa.* (Mwaona?)

Chotero iwo ali *pamaso pa mpandowachifumu wa Mulungu, ndipo akumutumikira iye usana ndi usiku mu kachisi:*...

202 Tsopano, nkuti kumene Akazi a Branham amanditumikira ine? Mu nyumba. Uyo ndi Mkwatibwi. Akazi a Neville, ndi kumene iwo amakhala, mu nyumba, kukutumikirani inu. Ndiko kumene Mkwatibwi ali, si antchito, Mkwatibwi.

...amatumikira...mu *kachisi: ndipo* iwo... *wakhala* pa *mpandowachifumu adzakhala* ndi *iwo.*

Ndipo *iwo sadzamva njala kenanso,*...(Iwo anaphonya zakudya zingapo, zimaoneka ngati (si choncho iwo?) pamene iwo anali kuno)...*sadzamva njala kenanso, ngakhalenso* iwo *kudzamva ludzu*... *ngakhalenso dzuwa silidzawalira pa iwo, kapena kutentha kulikonse.*

Pakuti Mwanawankhosa yemwe ali pakati pa iwo adzawatsogolera iwo ndi *kuwadyetsa iwo, ndipo adzawatsogolera iwo kumka* ku—ku *amoyo*...(miniti chabe)...*akasupe amoyo a* madzi: *ndipo Mulungu adzapukuta*...*misozi yonse* (ilo ndi gulu lolira limene linafika mmenemo) *yochokera mmaso mwawo.* (Mwaona?)

203 Tsopano, zindikirani, iwo ankamva njala ndi ludzu, ndi kumalira, ndi kubuula ndi kupempha, iwo anabwera kuchokera mu chisautso (ankati, "Tayang'ana pa gulu ilo la oyera odzigudubuza, o, iwo ndi openga!"). O, mai! Eya. Mwaona? Koma iwo ankalira ndipo iwo ankapempha, iwo sanali kukangana ndi kulundirana. Ndipo iwo ankangolira ndi kumapempha. Ndipo, onani, ndipo iwo anali mitundu yonse, malirime ndi mafuko.

204 Tsopano, handiredi ndi forte-foro sauzande, anali Ayuda. Abrahamu anali wantchito wa Mulungu. Ayuda akhala nthawizonse ali antchito a Mulungu. Amitundu sanayambe akhalapo antchito Ake.

205 Tsopano, tiyenera basi kuti tifulumire kudutsa mu izi tsopano, chifukwa ife tiri nawo awiri kapena atatu ena. Ndipo ine ndifulumira mwamsanga basi monga ine ndingathere, ndipo osati kuyesera kudutsa pamwamba pa izi. Koma ine ndidzabwerera ndi kudzawatenga iwo kachiwiri Lamlungu lotsatirali (ngati Ambuye alola) ndi kutenga nthawi yochuluka pa iwo.

206 Koma, penyani tsopano, iye anaona ngodya zinai zonse za dziko lapansi, ndi angelo ataima pa ngodya zinai za dziko lapansi. Tsopano, inu mukuti, "Ine ndimaganiza ilo ndi

lozungulira"; izo sizipangitsa ilo kuti lisakhale ndi ngodya zinai, inu mukuona. Chabwino.

207 Tsopano, "Pa ngodya zinai za dziko lapansi, atagwira mphepo zinai." Mwa kuyankhula kwina, apa pankapita mphepo, zikukupiza mwa nkhondo ndi makangano zimene zimadza pa dziko lonse. Kodi izo zinayamba zachitika liti? Kunalibe mpaka Nkhondo Yoyamba Yamdziko. "Atazigwira mphepo," ndipo iwo anali akulimbanira, kulowa umo kuti alilande.

208 Ndipo tsopano, apa akubwera Mmodzi wina. Tsopano, ngati inu mutapenya ndi kumutsatira Mngelo ameneyo, iye ndi Mngelo yemweyo amene anadza mu Ezekieli 9, pamene amuna anadza kuchokera kumbuyo kwa zipata zawo ndi zida zophera ndipo iwo anali kudutsa mu Yerusalemu kuti azikawapha Ayuda. Inu mukukumbukira? Iye anati, "Igwireni iyo! Igwireni iyo. Iyimitseni iyo, mpaka inu mutapita kudutsa mu mzinda ndi kukaika chizindikiro pa mphumi iliyonse omwe akuusa ndi kulira chifukwa cha zonyansa zimene zikuchitidwa mu mzinda." Ndi kulondola uko?

209 Ndiye, Iye atatha kuchita izo, ndiye Iye anawalola iwo kuti alowe umo ndi kukawapha. Chimenecho chinali chizunzo pansi pa Tito. Tsopano, inu mukuona, iye ndi Mngelo yemweyo, anabwera kachiwiri, akubwera kuchokera Kummawa (ndi kumene Yesu ati adzachokere) ndipo Iye anali ndi Chisindikizo cha Mulungu Wamoyo. Ulemerero!

210 Tsopano, kodi Chisindikizo cha Mulungu Wamoyo nchiyani? O, ngati icho sichiri mtsutsano waukulu mu dziko lero! Ena amati ndi kusunga tsiku la sabata, ndipo ena amati icho ndi kuchita *izi* ndi *izo*. Koma Baibulo linati "Mzimu Woyera ndiwo Chisindikizo cha Mulungu"! Aefeso 4:30 amati, "Musaukwiyitse Mzimu Woyera wa Mulungu umene inu munasindikizidwa nawo kufikira tsiku la chiombolo chanu." Mwaona? Chabwino. Ndi Mzimu Woyera.

211 Ndiye chikudza nchiani? Tsopano, penyani! O, pamene ine ndiganiza za ichi, mtima wanga umalumpha. Tsopano Iye anati, "Gwirani mphepo zinaizo mpaka," (mwakuyankhula kwina) "ife titasindikiza antchito a Mulungu wathu mu mphumi zao." *Antchito,* "Ayuda" (Yohane anatembenuka, anati, "Ine ndinaona handiredi ndi forte-foro sauzande atasindikizidwa apo.") Tsopano, mphepo zonse zinayamba umo, ndipo izo zikadakhoza kuphimba dziko ndipo nkhondo ya Armagedoni ikanachitika mu Nkhondo ya Dziko Lonse Yoyamba, koma . . .

212 Tsopano ine ndiyenera kuti nditenge Lemba lina pano kuti "ndikuonetseni inu. Yesu anayankhula za anthu kuti . . . Iye anati, Ena anadzamo pa ora limodzi, ndipo ena ora lina, ndipo iwo panali anthu a ora la leveni. Anthu a ora la leveni." Tsopano, inu amene muli auzimu muwerenge pakati pa mizere, chifukwa ine ndiyenera kuti ndilumphe pano nkufulumira. Tsopano,

penyani. “Kubwera umo, anthu a ora la leveni.” Ndipo tsopano pano . . . “Oyamba anabwera umo ndipo analandira khobidi, ndipo osatira analowa mkati ndipo analandira khobidi, ndipo anthu a ora la leveni analandira khobidi lomwelo lomwe iwo anatero a pachiyambi.” Ndi kulondola uko? Ora la leveni!

213 Tsopano, penyani, Myuda ndi chikhomo cha mtunda, womwe ife tiri kumutsatira iye tsopano. Tsopano, pamene Nkhondo Yoyamba, ya Dziko Lonse inadza, iyo inamutenga Myuda aliyense, iwo anabalalikira ku mafuko onse. Monga Lemba loyamba limene lero linafunsidwa, momwe Iye akanati adzawabalalitsire iwo pakati pa maiko onse, kumene iwo onse ali. Ndipo pano zikudza mphepo kubwera mu Yerusalemu, kulikonse, nkhondo ya dziko lonse.

214 Ndipo Iye anati, “Igwireni! Iletseni iyo, mpaka ife titasindikiza antchito a Mulungu wathu.” Mwa kuyankhula kwina, “Ife tiwabweretsa iwo umo kuchokera ku mafuko onse, kulikonse, kuwabweretsa iwo umo chifukwa ife tiyenera kuti tiwatengere iwo ndithu mkati umu kuti tiwasindikize handiredi ndi forte-foro sauzande aja. Igwireni iyo!”

215 Ndipo Nkhondo ya Dziko Lonse Yoyamba inaleka pa mwezi wa leveni wa chaka, tsiku la leveni mu mwezi, ora la leveni mu tsiku, kuti anthu a ora la leveni akanakhoza kubwera umo. Kuitanidwa kotsiriza kwa Myuda! Ndipo iye alandira ubatizo wa Mzimu Woyera womwewo umene iwo anaulandira kumbuyoko pa chiyambi kumbuyo uko pa Pentekoste, kubatizidwa mwa njira yomweyo, ndi chirichonse, anthu a ora la leveni kubwera umo.

216 Iye anati, “Igwireni iyo, tsopano, mpaka ife titasindikiza.”

“Ndi motalika bwanji Inu muti muigwire iyo?”

217 “Mpaka ife titawasindikiza antchito a Mulungu wathu. Tsopano, ife—ife tikuwasindikiza Amitundu, iwo akhala akusindikizidwa ndithu, zikwi kuchulukitsa zikwi kupyola mu zinzunzo izi ndi zisautso, iwo asindikizidwa ndithu. Koma dikirani miniti! Miniti yokha! Musati mulole a- . . . Musati mulole nthawi kuti ifike mpaka ife titawasindikiza antchito awa.” Ndipo iye anawasindikiza handiredi ndi forte-foro sauzande.

218 Ndiye mphepozo zinamasulidwa kachiwiri. Tsopano, zindikirani, ndipo kuyambira Nkhondo Yoyambayo ya Dziko Lonse kwakhala kuli mowirikiza chizunzo motsutsa Myuda. Kunauka Hitler ndi Nkhondo Yachiwiri ya Dziko Lonse, ndipo pamene iye anatero, iye anayamba ku . . . Kutani? Iye ankati aling’ambe dziko lonse mozungulira kumene. Ndi kulondola uko? Iye ankati aling’ambe ilo lonse, ndi kuzunguliza kumene. Inde, iye anatero.

219 Chirichonse chinkayenera kuti chikhale Chikominisi. Kodi inu mukukumbukira pamene iwo anakati andiike ine mu

ndende kumusi kuno? Ine ndinali kulalikira chinthu chomwechi kumusi uko mu Holo ya a Redman usiku uja. Inde, bwana. Ndinati, "Kudzakhala ma ismu atatu. Ndipo izo zonse zikanati zidzaunjikane mu ismu imodzi, ndipo ismu imeneyo ikanati idzabweretse chizunzo chimene chiti chidzamutumize Yesu Khristu ku dziko lapansi kachiwiri." Ndipo ziri ndendende chomwecho. Ndipo icho chinali Chikominisi, ndi—ndi Hitler ndi—ndi Nazi, ndi zina zotero; ndi momwe chi Fascismu cha Mussolini, ndi Hitler, ndi Stalin. Ine ndinati, "Chimodzi cha izo chidzatenga malowo. Ine sindikudziwa ndi chiti chimene chidzakhale, koma ine ndikukhulupirira idzakhala ili mfumu ya Kumpoto." Ndithudi inu mukuzikumbukira zinthu izo ndi momwe izo zakhala zikuphunzitsidwira mkati muno; ndipo M'bale Mahoney, ndi inu nonse kuchokera kutali mmbuyo umo, mukudziwa.

220 Ndipo iwo anati, "Ngati iwe uzilalikira izo . . . "

221 Ndi pa chinthu cha N.R.A. ichi, ine ndinati, "Icho si chilemba cha chirombo ayi, ndithudi ayi. Icho ndi kuwukira kwachipembedzo; osati izo." Ine ndinati, "Icho ndi chongotsogolera chabe kuti anthu apangitsidwe kukhala okonzeka, ndi kumadziwa kuti chiyambi ichi, pomwe pano ndi pachiyambi pa zachisoni, pomwe pano ndi pamene ife tikuyambirapo. Pomwe pano ndi—pamene nthawi ikuyamba kuti itsekeke. Tsopano, zindikirani, apo pa nthawi imeneyo."

222 Tsopano, chisautso chinadza pa Ayuda, ndipo iwo anayamba kumawazunza iwo kuchokera ku fuko lirilonse ndi kuwathamangitsira iwo mkati momwe mwa Yerusalemu. Ndi kulondola uko? Mmodzi aliyense, iwo akupita kumene . . . Ndipo Iye adzakhala nawo handiredi ndi forte-foro sauzande. Tayang'anani cha kuno mopitirira pang'ono mu Chivumbulutso pamene Yohane . . .

223 Bambo Bohanon kumusi kuno ananena ndi ine, anati, "Ine sindikanakhoza kuwerenga Chivumbulutso icho." Anati, "Apo panali Mkwatibwi ataimirira pa Phiri la Sinai." Anati, "Apo panali Mkwatibwi kutali uko Kumwamba." Ndipo anati, "Uko kunali Mkwatibwi, ndi madzi3chinjoka chikulavula madzi kuchokera mkamwa mwake kuti chipange nkhondo ndi Iye." Iye anati . . .

224 Ine ndinati, "Bambo Bohanon, chinthu cha izi, inu muli ndi chinthu cholakwika, mukuchitcha icho 'Mkwatibwi.'" Ine ndinati, "Ayuda adzaima pa Phiri la Sinai, handiredi ndi forte-foro sauzande. Mkwatibwi, molondola, anali Kumwamba ndi Yesu. Ndipo chinjoka chinali kulavula madzi kuchokera mkamwa mwake kumapanga nkhondo ndi *otsalira* a Mbewu ya mkazi." Ilo linali gulu *ili* kuno limene linkayenera kuti lipite uko, osati *ilo*. Mwaona? *Otsalira* a Mbewu ya mkazi, "mpingo

woyeretsedwa," opanda kulandira Mzimu Woyera, awo ndiwo amene iye anapanga nawo nkhondo. Mwaona?

225 Ndi awa pano, pali mafuko atatu. Nthawizonse muzisunga ma atatu awo mu malingaliro. Ndipo *pano* iye anaona, kuzungulira, handiredi ndi forte-foro sauzande awa atazungulira Mkwatibwi wamkulu woomboledwa uyo. Ndi otsalira awa anasiidwa ndi awo apo, ndi awo apo Ayuda, apo pali, osindikizidwa, handiredi ndi forte-foro sauzande. Pano pali iwo amene anayeretsedwa, amene anakana kuti alandire Mzimu Woyera. Mpingo udzazunza motsutsa . . . m—mpingo wa Chiroma ndi iwo adzawazunza awa. Koma Mkwatibwi wakwatulidwa kale ndipo ali Kumwamba. Uko iwo ali, akhazikitsidwa ndendende momwe Baibulo linati iwo akanati adzakhale ali. Mwaona?

226 Chotero handiredi ndi forte-foro sauzande awa ndi Ayuda, antchito a Mulungu. Ndipo pamene Uthenga wa Mzimu Woyera walalikidwa kwa iwo, ndipo iwo atalandira Ubatizo wa Mzimu Woyera ndendende basi monga ajawa ankachitira pa chiyambi, nyengo ya Amitundu yatsirizika, Mpingo wasindikizidwa, Mkwatulo wabwera.

227 Masiku a Amitundu, Uthenga walalikidwa paliponse, wakhomereredwa pakati pa Amitundu, kukoka khoka, kuyesera kuti atenge nsomba iliyonse imene ili mu madzi kuti idze umo. Ndipo tawayang'anani iwo, zazikulu . . . ? . . . Zokoledwazo zinali akamba onse ndi akangaude a mmadzi, ndi zina zotero. Basi mwamsanga pamene chitsitsimutso chitha iwo amapita kubwerera mmbuyo momwe kupita mu dziko kachiwiri. Nsomba pafupifupi zawedzedwamo kale. Mukuona chimene ine ndikutanthauza?

228 Uthenga walalikidwa! Inu simukumva kulira kwinanso ayi, palibe kubuula kwinanso, palibe ayi, kuusamoyo kwina ayi, kulirira ubatizo wa Mzimu Woyera. Iwo amakonda kuti adze umo, eya, iwo amaika manja awo pa iwo mwa mazana, ndipo iwo amapitiriza ndi kumavina, mwina, kapena chinthu china chonga izo. Izo zonse ndi zabwino, koma izo ndi zotsatira chabe.

229 Munthu Khristu Yesu amabala chinthu chenicheni, ndipo amamusunga munthu ameneyo wotetezedwa mwa Khristu mpaka Iye abwere. Ndi Uyo apo. Ndipo tsopano, ndipo izo ndi pamene kulibe kulira kwinanso, zitseko zangotsala pafupi kutsekedwa. Nkhoka yapita kumene, iyo ili pafupi nthawi yake yotsiriza, ochepa okha kuti akoke izo monga choncho kuti alowe mu Ufumu wa Mulungu. Zitseko zikutsekedwa!

230 Ndiye chinthu chotsatira ndi chiani? Ayuda ayenera kuti alandire Mzimu Woyera ndi kuti abatizidwe mu Dzina la Yesu Khristu. Nthawi yonseyi iwo amamuzunza ndi kumunyogodola; ndipo, kumeneko, mwamsanga pamene Mzimu Woyera uti udzaperedwe kwa iwo, iwo adzalandira ubatizo wa Mzimu

Woyera. Mpingo wa Amitundu wakwatulidwa. Ndipo iwo amene anaukana, ndi kumangoyenda pansi pa kulungamitsidwa, chinjoka (mphamvu ya Chiroma) chikulavula madzi, pamene agwirizana ndi Chikominisi, ndipo akuutengera mpingo mu chizunzo monga choncho. Apo iwo akujambulika ndendende.

231 O m'bale, pamene ife tikuziona izo zikubwera, ndi chifukwa ine ndikupemphera, ndi chifukwa ine ndikulirira kwa Mulungu, "Ambuye, ine ndikufuna ndikafike kwa Ayuda awo. Mundirole ine ndikayambire kumusi uko mu Afrika, ndikagwire ntchito ndi owerengeka a Amitundu ndi Achimuhamadi. Ndipo mundirole ine ndidzapite uko mu India ndi kukayesera kuzichita ndi kuonetsera kwa iwo Ambuye Yesu Khristu weniweni ndi mphamvu Zake, zozizwitsa Zake, Ubatizo Wake, chirichonse, ndi Mzimu Woyera." Ndiye pamene iwo akafike ku Yerusalemu . . .

232 M'bale Beeler, ichi chiri pa zomwe iwe unali kuzifunsa. Pamene iwo akafika ku Yerusalemu ndi kukaima kumeneko, ndi kukati, "Tsopano, ngati Yesu ali Mwana wa Mulungu amene anauka kwa akufa, Iye amadziwa zinthu mofanana monga Iye ankachitira mmbuyo uko pachiyambi, Iye akhoza kubala Moyo womwewo umene Iye ankauchita mmbuyo uko. Ndipo ngati Iye angatero, kodi inu mumulandira Iye ngati Mpulumutsi wanu?" Ndiyeno nkuonetsa kuti Mulungu ndi mphamvu Zake zazikulu ndi zinthu za mphamvu ya chiukitsiro Chake, Iye ali ndi ife.

233 Ndiye pamene iwo adzachita izo, nkuti, "Tsopano, inu amene mwamulandira Iye ngati Mpulumutsi wanu . . ." Ine ndikuyembekeza adzakhala ali zikwi za iwo. Nkuti, "Mzimu Woyera womwewo umene unagwa pa Tsiku la Pentekoste ali pomwe pano kwa inu."

234 Ndiye Uthenga ukubwereranso kwa Ayuda pomwepo pa nthawi imeneyo. Ndiye kudzakhala kuli chitsitsimutso pakati pa Ayuda awo kumeneko chimene chiti chidzanyamule zikwi ndi makumi a zikwi ndi . . . handiredi ndi forte-foro sauzande, kulowa mu Ufumu wa Mulungu, adzasindikizidwa ndi Mngelo wosindikiza.

235 Ine ndikudalira kuti Iye akubwera kuchokera Kummawa. Uko ndi kumene Iye ali pochokera kwa ife tsopano, ali ndi chisindikizo Chake mu dzanja Lake. Ndiye, o, ine ndikufuna kuti ndikasonkhanitsidwe mmenemo. "Ine ndatumiza chisautso kuno ndi chisautso uko, ndipo ine ndawathamangitsa Ayuda ndi kuwathamangitsa iwo molimba monga ine ndikadathera. Ndipo iwo ayenda kubwerera mmbuyo. Ayuda ambiri ali mu United States (momwe iwo sadzatha kudzathawamo) alandira kale Mzimu Woyera. Koma ine ndiri nawo handiredi ndi forte-foro sauzande onse ataimirira uko amene ati adzalandire ubatizo wa Mzimu Woyera."

236 Ndipo apo pomwe, mwamsanga pamene Mngelo wosindikiza uyo akuyamba kuwasindikiza handiredi ndi forte-foro sauzande, chitseko cha Mpingo wa Amitundu chatsekedwa, ndipo Ayuda akutengera Mzimu Woyera kwa Ayuda. Ndipo iwo adzakhala ndi chitsitsimutso chimene chiti chidzasese dziko lonse. Aleluya! Ndipo mphamvu ya Mulungu idzaonetseredwa pakati pa Ayuda. O, ndi zodabwitsa bwanji! Fyuu! O, mai!

237 Ndiroleni ine ndione, mwamsanga ndithu, "Yesaya . . . " Ife tawatenga "ana a Mulungu" aja. Tsopano tiyeni tione:

Kodi Israeli . . .

238 Onani ngati inu mungakhoze kuziwerenga izo, m'bale. Ine . . . Ilo limakhala ngati limayendera limodzi, iye analifufuta ilo nthawi zingapo. Ndipo ine ndifunefune lina. Ngati inu mungalole, chonde [M'bale Neville akuwerenga funso lotsatirali—Mkonzi.]

14. Kodi tanthauzo la Yesaya la "kusula kwa malupanga kukhala makasu," zidzafika podzachitika mu ulamuliro wa zaka-chikwi-chimodzi wa Khristu, kusiyana ndi chinachake chimene munthu akhoza kubweretsa monga zipembedzo zochuluka zambiri zamakono zimatiuzira ife?

239 Yense yemwe inu muli, m'bale wanga wokondedwa kapena mlongo . . . zikuoneka ngati zolemba za mwamuna. Koma, mulimonse, yense yemwe inu muli, inu mukulondola ndendende! Ndi pamene makasu olimira adzasulidwa . . . kapena pamene malupanga adzasulidwa kukhala makasu olimira. Izo zidzabweretsa Ulamuliro wa Zakachikwi. Ndipo mipatuko yonse iyo yachipembedzo yamakono imene ikupita mozungulira kumayesera kuwaphunzitsira anthu mu Ufumu wa Mulungu . . . Izo zidzakhala pamene Mulungu Mwiniwake adzabwera mu Uthunthu wauzimu ndi mu Mphamvu yauzimu, kwa anthu okhulupirira-zauzimu, ndipo adzalandira Mphamvu yauzimu imene iti idzawaumbe ana a Mulungu. Aleluya! Uko sikudzakhala konse kuwerenga, kulemba, masamu, izo zidzakhala mwa mphamvu ya chiukitsiro cha Yesu Khristu. Ndiye dziko silidzaphunzira nkhondo aponso.

240 Fuko lirilonse lero, mphamvu iliyonse, ufumu uliwonse, ukulamulidwa ndi Mdierekezi. Baibulo limanena choncho. Ndipo limodzi la masiku awa ufumu wa dziko lino udzakhala maufumu a Ambuye wathu ndi a Khristu Wake, ndipo Iye adzawalamulira ndi kuchita ulamuliro zaka chikwi pa dziko lapansi; ndi kuukwatula Mpingo. Ndendende, ndiko kulondola ndendende, muwerengi wokondedwa.

241 Handiredi ndi forte-foro sauzande ndi antchito. Chiwerengero chachikulu chimene palibe munthu akanakhoza . . . "Unyinji umene palibe munthu akanakhoza kuwuwerenga," ndi Amitundu.

242 Miniti yokha tsopano, kanthu kamodzi kena kakang'ono apo. Ine sindingakhoze. Ine ndidzangokhala ndi kupemphera kwa osonkhana ndiye, mu maminiti pang'ono. Penyani apa, ine ndikuganiza Ichi ndi chofunika kwambiri pakali pano. Ine ndikufuna kuti ndipempherere odwala, koma ife tifulumira. Mmalo mokhala ndi kuzindikira za mumtima, ife tingopita modutsa basi. Ine ndikufuna kuti ndikufunseni inu chinachake. Panopali ngakhale limodzi lina. Ine ndingotenga ili ndi kudzalitenga ilo Lamlungu lotsatira, ine ndikuganiza.

243 Taonani, abwenzi, pa ichi, kukongola kwake! Penyani! Ndikufuna inu kuti muyang'ane tsopano, mwatcheru, munthu uyu amene anafunsa funso ili. Handiredi ndi forte-foro sauzande, tsopano, awo ndi antchito, iwo azidzatumikira. Ngati inu munazindikira, mwamalo, mu Lemba lakale . . .

244 Nthawizonse muziyang'ana pa mthunzi ngati inu mukufuna kuti muone chomwe chenicheni chiri. Ndiko kulondola. Muziyang'ana mmbuyo uko, onani chomwe chiri. Tsopano, ndizo mosinthanitsa kuyambira pa Mtanda, ndipo yang'anani chomwe chenicheni chiri ngati inu mukufuna kuti muone chomwe mthunzi uli. Kumbuyo uko, icho chinali kupendekera mpaka ku Mtanda, ife tinkayenera kuti tiyang'ane (kumbuyo uko) kuti tione mthunzi, kuti tione chomwe Mtanda ukanati udzakhale uli; tsopano inu muyenera kuti muziyang'ana kuchokera ku Mtanda, kuti muyang'ane mmbuyo ndi kuona chomwe mthunzi uli. Mwaona? Yang'anani chomwe Khristu anali mu masiku amene Iye anali pano pa dziko lapansi, chomwe Iye anali apo Iye ali tsopano. Uwu ndi mthunzi Wake. Mukuona chomwe ine ndikutanthauza? Inu mukudziwa, pachiyambi pamene ine ndinalongosola izo, ndi chimene chiri. Tsopano, ngati ine ndikuyang'ana kuchokera kumbuyo uko, ine ndimayenera kuti ndiyang'ane chomwe mthunzi unali kuti ndipeze chomwe ichi chikanati chikhale, chomwe Mtanda unali.

245 Tsopano, tsiku lina munali tchimo mu Israeli, ndipo kunali munthu . . . wa fuko lotchedwa Levi. Iwo anasolola malupanga awo ndipo iwo anapita ndi Mose ku msasa, ndipo iwo anaononga chirichonse chimene chinali tchimo. Ndi kulondola uko? Mulungu anayang'ana pansi ndipo anati, "Chifukwa inu mwachita izi ndipo munandiimira Ine, anu . . . ena onse awa azikutumikirani inu. Ndipo inu mupite mu kachisi momwe ngati ansembe." Nkulondola uko? "Inu muzikhala mu kachisi momwe, ndipo ena onse a iwo azigwira ntchito ndipo azibweretsa umo chakhumi ndi kumakusamalirani inu." Nkulondola uko?

246 O, aleluya! Ngati inu mungakhoze kuona chomwe kachisi uja anali, kuti Alevi anali Mkwatibwi. Tsopano, pamene tchimo likubuka pa dzanja lirilonse, Alevi akusolola malupanga awo. Mkwatibwi wobadwa mwa Mzimu Woyera akuimirira panja, akuti, "Yesu Khristu mwa chenicheni ali Yesu Khristu mu mthunzi, mofanana basi. Tchimo likadali tchimo, ndi zolakwika

kumachita zinthu izi!" Ndiko kulondola, iwo aimirira pamenepo ndi Lupanga.

247 Mulungu akuti, "Bwerani inu tsopano, odalitsidwa ndi Atate Anga." Amenewo ndi Mkwatibwi.

248 Awo ndi antchito, ndipo yang'anani kumene antchitowo ankamanga misasa. Khumi ndi awiri ku mbali iyi. . . Ine ndikutanthauza, anai ku mbali *iyi*, anai ku mbali *iyo*, anai ku mbali *iyo,* ndi anai ku mbali iyo; mafuko khumi ndi awiri. Mafuko khumi ndi awiri ndiwo handiredi ndi forte-foro sauzande. Tayang'anani mu Bukhu la Chivumbulutso, iye anaona Mzinda uli ndi maziko ake khumi ndi awiri. Pa chipata chirichonse panali dzina la mtumwi, ndipo zipata khumi ndi ziwiri. Ndipo kuzungulira iwo panali mafuko khumi ndi awiri, (aleluya!), atakhala mozungulira.

249 Ndipo mkatimo munali Owomboledwa. Aleluya! Akuda, oyera, achikasu, abulauni, ndi onse amene ali otsukidwa-Mmagazi adzakhala antchito Ake. Iye anati iwo adzakhala limodzi ndi Iye. Iwo adza. . . Dzuwa silimadzawamba pa iwo aponso, iwo sadzamva njala kapena ludzu aponso, ndipo kupyola M'badwo waukulu wosatha iwo adzakhala moyo ndi kuchita ufumu ndi Khristu kosatha: Iye, Mfumu; ndi iwo, Mfumukazi. Adzalamulira ndi kuchita ufumu kosatha!

250 Ambuye akudalitseni inu. Ameni. Ine ndiwasunga awa; Mulungu akalola, ine ndibwerera kumene ndi iwo kachiwiri, mwina usikuuno, ndi kudzawayankha iwo usikuuno kapena paliponse M'bale3ife titi tidzabwere pamodzi ndi kudzayankhulana. Ambuye akudalitseni. Inu mukumukonda Iye ndi mtima wanu wonse?

O, ndifuna kumuona, kuyang'ana nkhope Yake,
Kukakhala mwa chisomo chopulumutsa;
Pa njira za Ulemerero nkakweze mau anga;
Zonse zatha, ndiri kwathu, mosangalalabe (O, mai!)
Pakuyenda dzikoli, kuimba ndikupita,
Kulozera miyoyo, ku mwazi woukha, (osati—osati ku mpingo; ku Gologota.)

251 Ndiko kumene ife tikulozera; osati ku zamulungu zina, koma ku kuukha koyeretsa, kwa Yesu Khristu. "Moyo uli mu magazi," ndipo Iye ndiye Mwazi wa Mulungu umene uli Moyo wathu umene ukukhala mwa ife tsopano. Chodala chikhale chimango chimene chimamangiriza!

252 Pamene ife tikuti tizipempherera odwala, ine ndikufuna y—yapadera pakali pano. Ine ndikufuna Mlongo Gertie ndi mwana wake wamkazi, ngati iwo angatero, kuti abwere kuno. Ndipo iyi ndi nyimbo yapachiyambi yachikale, ine ndikufuna inu kuti muzindiimbira ine iyo, *Kungokhulupirira.*

Ine ndikukumbukira, ndinali ndikulowa pa khomo apo, ndipo nyimbo imeneyo yandilondola ine konse kudutsa mafuko. Ndipo ine—ine ndikufuna iwo kuti ayiimbe, iye anali woyamba kuyiimba iyo, woyamba amene ine ndinamumva. Bwanawe wanga anailemba iyo, Paulo Rader. Ndipo, ife tisanapempherere odwala, ine ndikufuna iwo kuti aziyiimba iyo pamene madalitso a Mulungu akukhazikikila pa anthu kwa odwala.

253 Ife tatenga nthawi yochuluka. Pepani, M'bale Neville. Mulungu akudalitseni. Kodi inu mukuwakonda mafunso? Ine ndiri. O, ndipo awo anali abwino zedi, iwo anali abwino kwambiri basi. Ndipo pali basi mulu wina. Ndipo, kwenikweni, ena a iwo sanadutsidwemo panobe, o, pangokhala ochuluka kwambiri kuti tidutse mwa iwo. Ambuye adalitse ndithu.

254 Nonse a inu ikani malingaliro anu pa Khristu tsopano, ndipo tiyeni tisinthe kuchokera ku mafunso tibwerere ku machiritso Auzimu. Ndi angati ali muno kuti apemphereredwe? Tiyeni tione manja anu, akufuna kuti apemphereredwe. Chabwino, ife tiwabweretsa iwo apa ndi kuwapempherera iwo mu mphindi yokha, pamene alongo athu aziyimba nyimbo yokongola iyi. Pamene iwo ali kukonzekera, lapachikika pamwamba pa inu pomwepa tsopano ndi Lonjezo, ili ndi Baibulo Lake. [Mlongo Gertie ndi mwana wake wamkazi akuyimba *Ingokhulupirira*—Mkonzi.]

Khulupirira, khulu . . .

255 Tsopano, inu amene mukudwala, sunthirani kuno kuzungulira guwa tsopano, ngati inu mungathe.

Zonse ndi zotheka, khulupirira;
Khulupirira, khulupirira,
Zonse ndi zotheka, khulupirira.

256 [M'bale Branham akuyamba kung'ung'uza *Ingokhulupirira*—Mkonzi.] Tsopano, Atate Akumwamba, ndife othokoza kwambiri lero chifukwa cha Lemba ili ndi chifukwa cha nyimbo iyi, "Ingokhulupirira." Ife tikukhoza kukumvani Inu mukunena kwa bambo yemwe anali wakhunyu, "Ingokhulupirira kokha, pakuti zinthu zonse ndi zotheka."

257 Tsopano, ife tikupemphera, Mulungu, pamene anthu awa akubwera ku guwa kuti adzapemphereredwe, kuona kuti ife tiri pano, mwamthunzi, mthuzi chabe; chenichenicho chiri potizungulira ife basi, Mzimu wachisavundi umene unali pa ife sudzafa konse. Iwo udzakhalapo kudutsa mibadwo yosatha yonse. Ndipo ife tikupita tsopano monga wantchito Wanu wodzozedwa, kuti tiwathandize anthu amzathu kuti alandire chithandizo, pa chosankha chimodzi chokha, Atate, ndicho kuti iwo akanati azikutamandani Inu. Ndipo tsopano mulole aliyense waima pano pa guwali mmawa uno, wodwala, wovutika, tsopano mulole Mzimu Woyera upereke machiritso kwa aliyense wa iwo.

258 Ndipo ife monga kagulu kakang'ono—kakang'ono, komwe alongo anali kungoimba za iko, "Musaope, nkhosa zapang'ono," ife tikudziwa, Ambuye, ndi chifuniro Chanu chabwino kuti mupereke Ufumu kwa iwo. Ndipo ife tikudziwa kuti Inu nthawizonse muli pafupi, pakuti Inu munati, "Kulikonse kumene awiri kapena atatu adzasonkhana mu Dzina Langa, Ine ndidzakhala ndiri pakati pawo. Ndipo chirichonse chimene iwo achipempha, Ine ndidzapereka icho."

259 Tsopano, molingana ndi Mawu a Mulungu amene sangakhoze kulephera, Mawu a Mulungu, perekani machiritso kwa aliyense, Ambuye. Ndipo iwo akuimirira pano, akuyembekezera. Pamene ife tikupita kuti tikawadzoze ndi mafuta ndi kuika manja pa iwo, ndi kuti tipemphe chiombolo, mulole aliyense wa iwo apite ku mipando yawo, kubwerera ku makwao, akukutamandani Inu, (abwinobwino, angwiro, ndi ochira), ndi kukabwerera kachiwiri usikuuno, Ambuye, ku msonkhano, akupereka matamando ndi ulemerero kwa Mulungu chifukwa cha machiritso awo. Perekani izi, Ambuye.

Ndipo ife mitu yathu ili chiweramitsire:

260 M'bale Neville, bwerani nane, ngati inu mungatero. Ine ndikufuna M'bale Fleeman, ndi M'bale Deitzman, kapena winawake pano, ndi M'bale Cox, inu nonse mubwere kuno ndi kudzandithandiza ine pa guwa. Madikoni muno a mpingo ndi amene ine ndikuwaitana pa nthawi ino.

261 Ndipo pamene ife tikuwapempherera iwo, inu mukhoza kumawathandiza iwo ngati inu mukufuna. Ine—ine ndikufuna aliyense muno kuti akhale wotsimikiza kwenikweni. Ndipo pamene ife tizipempherera odwala, ine ndikufuna inu kuti muzipemphera limodzi nafe.

262 Ine ndikuona mnyamata wamng'ono wakhala kumbuyo uko tsopano, amene kanthawi kapitako anatuluka kunja kwa holo umo ndipo anali ndi kutaya kwa magazi. Ndipo Ambuye Yesu modabwitsa kwambiri analeketsa magaziwo pomwe pano. Mwaona? Chifundo chake chiyamikike, Dzina Lake lilemekezeke. Ingoonani ambiri omwe achiritsidwira mu masiku owerengeka apitawa!

263 Tangoganizani, Ambuye Yesu yemweyo amene anali kumbuyo uko mu masiku a atumwi ali pomwe pano tsopano. Ndipo ziri kungotsiriza mathero a Amitundu. Kusuntha kwakukulu kukuchitika pakati pa okhulupirira zauzimu, chifukwa ife tikukhulupirira kuti Mulungu ali pano.

264 Tangoganizani, thupi lanu—lanu laulemerero liri komwe kuno ku Kachisi tsopano, Kukhalapo kwa Mzimu Woyera umene *uli* chikhalidwe chanu chaulemerero. Inu muli opatsidwa ulemerero mwa Khristu pakali pano! "Iwo amene Iye anawalungamitsa, Iye anawapatsa ulemerero." Ndipo thupi lanu lomwe laulemerero likuima pafupi ndi inu pakali pano,

mwa Khristu Yesu, kuti lipereke kwa inu nyonga monga nyese yopita mu batire. Mzimu Woyera uli mwa inu. Ndi woti upereke nyese kwa thupi lanu kuti ukupatseni inu nyonga zatsopano, kuti zikuchiritseni inu ku matenda amene inu muli nawo, kuti zikupangitseni inu kuchira.

265 Tsopano, ine ndikufuna mpingo, ngati iwo angatero, ndi alongo athu, ngati iwo aziimba nyimbo ija motero kachiwiri. Tsopano, aliyense wa inu pa guwa . . .

266 Tsopano, abwenzi, ngati ine ndiri wonyenga, ndine wosadziwa kuona kwake. Ine ndikuyesera kuti ndikhale Mkhristu, ndipo ndi mtima wanga wonse ine ndikuyesera kuti ndiziwathandiza anthu. Ndipo ine ndikuyesera kuti ndizikuthandizani inu, ana a Mulungu. Ndipo ngati ine—ngati ine ndikuwakonda Atate anga Akumwamba, ine ndizikukondani inu, ana Ake. Ngati ine sinditero . . . Ngati ine ndikukunyengani inu, ine ndayesera kumamunyenga Mulungu, inu ndinu ana Ake; palibe yemwe angakhoze kumunyenga Mulungu. Ine ndikuyesera kuti ndizikuthandizani inu.

267 Ndicho chifukwa Mulungu akudalitsa kulimbikira kwanga. Ndipo mwina ndi osauka kwambiri, ndipo kwina kwa iko ine ndikuchita nako manyazi, ndipo Mulungu akudziwa ine ndikuchita nazo manyazi ndi kulapa pa kulimbikira kwanga. Koma ine ndikuchita zonse zimene ine ndingakhoze kuti ndizithandiza Ufumu wa Mulungu ndi kumakuthandizani inu ana a Iye. Mulandireni Yesu mmawa uno ngati Mchiritsi wanu, pano pomwe pa nsanja, inu mubwerera ku mipando yanu ndi ku nyumba kwanu ndi kukhala abwinobwino ndi ochiritsidwa.

268 Tsopano, ngati Iye ati awachiritse mazana pano, ndi zikwi ndi zikwi kuzungulira dziko, angalekerenji Iye kukuchiritsani inu? Mungokhulupirira basi. Chabwino, alongo. M'bale Neville, ine ndikufuna inu kuti mubwere ndi kumadzawadzoza iwo. [M'bale Branham ndi abale akupempherera odwala. Mlongo Gertie ndi mwana wawo akuimba, "Kungokhulupirira."—Mkonzi.] . . . ? . . .

54-0103M Mafunso ndi Mayankho #1
Branham Tabernacle
Jeffersonville, Indiana U.S.A.

CHICHEWA

©2009 VGR, ALL RIGHTS RESERVED

VOICE OF GOD RECORDINGS, MALAWI OFFICE
P.O. BOX 51453, LIMBE, MALAWI

VOICE OF GOD RECORDINGS
P.O. BOX 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.
www.branham.org

Chidziwitso kwa ofuna kusindikiza

Maufulu onse ndi osungidwa. Bukhu ili mukhoza ku printa kunyumba kwanu ngati mutafuna kuti mugwiritse ntchito inuyo kapena kuti mukawapatse ena, ulere, ngati chida chofalitsira Uthenga wa Yesu Khristu. Bukhu ili simungathe kuligulitsa, kulichulukitsa kuti akhalepo ambiri, kuikidwa pa intaneti, kukaliika pakuti ena azitengapo, kumasuliridwa mu zinenero zina, kapena kugwiritsidwa ntchito ngati njira yopezera ndalama popanda chilolezo chochita kulembedwa ndi a Voice Of God Recordings®.

Ngati mukufuna kuti mumve zambiri kapena ngati mukufuna zipangizo zina zimene tiri nazo, chonde mulembere ku:

VOICE OF GOD RECORDINGS, MALAWI OFFICE
P.O. BOX 51453, LIMBE, MALAWI

VOICE OF GOD RECORDINGS
P.O. BOX 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.
www.branham.org